

# *KULIZINDIKIRA TSIKU*

## *LANU NDI UTHENGA WAKE*



Mmawa wabwino, abwenzi. Tiyeni tikhale chiyimire kwa mphindi yokha.

Wokonedwa Mulungu, pamene ife, mu chipwirikiti ichi ndi zolemetsa za moyo, tikuimikira kwa mphindi zotsatira izi kapena ora, chirichonse chimene chingakhale, chimene Inu mwatipatsa ife, kuti tipereke matamando ndi ulemelero kwa Inu, kuti tilalikire Mawu Anu, kuti tikudziweni Inu bwinoko, ndi chifukwa chake ife tasonkhana mmawa uno. Ife tikukuthokozani Inu, Mulungu, chifukwa chakuti alipo anthu amene ali okonzeka ndipo adzikonzekeeretsa okha kuti abwere adzamvetsere. Mosalabadira nyengozi ndi nthawi, ndi momwe ife tikukhalamo, iwo akukhulupirirabe. Ndipo ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha iwo.

<sup>2</sup> Mulungu, ndife oyamikira kwa Inu chifukwa cha mphamvu Yanu yayikulu yochiritsa, malonjezo a Mawu Anu. Momwe mitima yathu imatenthekera pamene timva maumboni awa! Mitundu yonse ya zosautsa zomwe zabweretsedwa pa ana a anthu! Inu, ndi chisomo Chanu ndi mphamvu, ndi lonjezo Lanu, mwawachiritsa iwo. Ndipo iwo ali pano, akuchitira umboni, akupereka matamando kwa Mulungu. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha zimenezi.

Ndipo tsopano mulole ife, lero, timve Uthenga umene Inu mwawupereka kwa ife kwa ora lino. Pamene ife tikuwerenga mu Mawu Anu, Inu mupereke kwa ife nkhani ya zomwe ife tikuziwerenga. Mulole chifuniro Chanu chichitidwe mu zinthu zonse, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

Mukhoza kukhala pansu.

<sup>3</sup> Ndi mwayi kukhala pano mmawa uno. Ndine wokondwa kwambiri chifukwa cha inu nonse. Ndipo M'bale Wood, M'bale Roy Roberson, abale ena ambiri, agwira ntchito mokhulupirika masiku awiri apitawa, kuti ayike mpweya wozizira mchipinda chino kwa cholinga ichi, chifukwa Lamlungu lapitali iwo anawona momwe inu munavutikira. Ndipo iwo anali ndi ndalama pang'ono mthumba la tchalitchi, ndipo anapita kukagwira ntchito ndipo aziyika izo kuti zigwire ntchito kukupangani inu kuti muzikhala omasuka, ndi ndalama zimene mumaziyika mu chopereka, pamene muzikhala pansu, mukumvetsera Uthenga. Mwazizirako kwambiri lero kuposa momwe mwakhala muliri. Chotero ndife oyamikira kwa Mulungu, ndi kwa anthu inu, chifukwa cha mwayi uwu.

4 Wokondwa . . . M'bale Roy Borders, iye amafuna kuti akhale ngati wakhala kumbuyo mmawa uno. Ndipo ndinamuuza iye kuti atenge mpando wake ndi kudzakhala kuno ndi atumiki awa, koma iye sanachite zimenezo. Monga inu nonse mukudziwa, M'bale Borders amatiimira ife mminda. Wokondwa kwambiri kukhala ndi M'bale Borders kuno, ndi atumiki ena ambiri ndi abwenzi.

5 Kudutsa msabatayi ine—ine ndinayamba kuganiza, ndikuti, “Ine ndikakafika kumeneko, Lamlungu, ine ndikamuzindikira mtumiki aliyense, munthu aliyense.” Ndiye iwe ukafika kuno, iwe umangotengeka kwambiri mu Uthenga mpaka iwe umangoyiwala chirichonse, pafupifupi, kotero chimene icho chinali.

6 Tsopano ine ndikuyenera kuti ndibwerere ku Arizona. Ine ndikuyenera kuti ndibwerere Lolemba likudzali, sabata, kubwerera ku Tucson, kuti ndikawatengere ana kumeneko ku sukulu. Ndipo ndidzakhala ndikubwereranso zikakatha zimenezo. Ndipo mkazanga ayenera akakhale kumeneko molawirira, kuti akayambe . . . kulembetsa ana, masabata awiri sukulu zisanayambe. Ndipo ine, kenako, ine ndizidzabwerera kwa kanthawi kuno.

7 Ndipo tsopano ino ndi nthawi yanga ya tchuthi. Monga inu mukudziwira, ndalalikira kuyambira Disembara; Januware, Februware, Marichi, Epulo, Meyi, Juni, ndi Julaye. Tsopano, ngati Mulungu alola, osati kuyitana kwapadera kulikonse, ino ndi nyengo imene ine—ine—ine ndimapumula, tchuthi changa. Ndimapita kukasaka. Ndipo ine . . .

8 Tsopano ngati Ambuye adzandiyitanire ine ku chinachake, zinthu zimenezo sizidzakhhalapo pa chithunzicho. Mulungu nthawizonse amakhala woyambirira. Ndipo ine ndimafuna kuti Iye azikhala woyambirira, ndipo inu mumafuna kuti Iye azikhala woyambirira. Komano ngati sipakhala kuyitana kotsimikizika, ndipo icho nkukhala chifuniro Chake, icho ndi chimene ine ndikuyenera kuti ndichite tsopano kwa miyezi ingapo yotsatirayi, ndi kupita kukasaka tsopano, kuti ndikazipumitse ndekha. Ine . . .

9 Inu simukuzindikira, dziko silizadziwa konse, zimene ndimayenera kuti ndidutse nazo. Mukuona? Ndipo izo zimangokhala kupsyinjika koteroko. Nzosadabwitsa kuti Ambuye anawauza ophunzira Ake, pamene Iye ankayenda ndi iwo, “Patukirani pambali mchipululu, mudzapumule kanthawi.” Mukuona? Ine ndikumazindikira zimenezo mochuluka, tsiku lililonse, ndipo makamaka pamene masiku anga akuchulukira pa dziko lapansi, inu mwaona. Pamene ine ndikukula, iwe umazindikira zimenezo. Inu mwawamva abusa athu akuti “ameni” kwa zimenezo, nawonso. Iye, ife, tikhoza kuzindikira

kuti sindifenso anyamata tikadutsa zaka fifite zakubadwa. Tsopano ife tikuyenera kuti tizikhala ndi kanthawi pang'ono.

<sup>10</sup> Ndife othokoza kwambiri chifukwa cha maumboni omwe tangowamva kumene. Mkazanga anali uko kwa Akazi a Wood, dzulo, pamene anthu ena anabwera kuchokera kumusi mu Alabama, kwina kwake kumusi uko, ndipo amakamba za zinthu zazikulu zimene Ambuye anachita mu msonkhano umenewo, za ana aang'ono akuchiritsidwa, ndi zinthu zosiyanasiyana. Ndi zinthu zambiri zimene, mai, izo zingangotenga nthawi yaitali kuti—kuti zinedwe.

<sup>11</sup> Ndiye inenso ndikuyenera kukumbukira kuti... Ine ndikukhulupirira ena a iwo anandiuza ine kuti Mlongo Larson wakhala ali kuno ma Lamlungu awiri ndi mwana wamng'ono. Ine sindingadziwe, koma ine ndikukhulupirira iwo anati uyo anali mdzukululu wake, mwinamwake, kudzadalitsidwa, kumubweretsa iye kuchokera ku Chicago. Donayo wakhala akutikomera mtima kwambiri ife, ndipo ife tikumuyamikira iye. Ndipo iye anabweretsa mwana wamng'ono kuchokera ku Chicago, kuti adzadalitsidwe. Chimene, iye ali ndi nthawi yochepera kuti amutulutse iye, ndikuganiza, kuti adzadalitsidwe, koma iye ali ndi chidwi ndi mwana uyu kuti aperekedwe kwa Ambuye. Chotero ngati Mlongo Larson angatero, pamene ine ndikuyankhula, ngati iye angamubweretse mwana ameneyo ku utumiki womudalitsa uwu.

<sup>12</sup> Ndiyeno, mwinamwake, pamene iye akukonzekera, ine—ine ndikufuna kunena kuti uwu wakhala Uthenga wovuta kwambiri umene ine ndinayamba ndayerapo kuwukonzekera, kufikira usiku wathawu. Kudutsa mu sabata, ine ndimapita mchhipinda, kuti ndikayesere kukakhala pambali nditathana nawo mafoni anga ndi zinthu, kuti—kuti ndiyesere kupeza chinachake mmalingaliro anga kwa ora. Ndipo ine ndikapita, ine—ine ndimalephera nkomwe... Maganizo anga amakhala opanda kanthu. Ndipo, dzulo, ine ndinapita mchhipinda chapansi. Ine ndinaganiza kwatentha kwambiri, kotero ine ndinatsikira kupansi mchhipinda chapansi, kukakhala pansu kumeneko. Ndipo ine ndimayesera kutenga Baibulo langa ndi kumawerenga, ndipo ndimagona. Kenako ndimadzuka ndi kumwa madzi, ndi kuyesetsa kumadzigwedeza ndekha, ndi kutuluka panja ndi kumakayendayenda, kukhala pa masitepe.

<sup>13</sup> Winawake anabwera ndipo anadzandipeza ine nditavula malaya anga, nditakhala pa sitepe; kunali kukulentha kwambiri. Iwo anadzandibaibitsa. Ine sindinadziwe ngati iwo anabaibitsa... Winawake, mwina anali winawake kuno kwathu kuno mu mzinda, kapena mwinamwake anali winawake mu tchalitchi, anadzandibaibitsa ine. Ndipo ine—ine ndinali ndikulungalira, ine—ine ndinangopezeka ndikuyang'ana pa galimoto, imadzutsa. Ine ndinabaibitsa.

<sup>14</sup> Usiku watha ine ndinalowa mgalimoto ndipo ndinakwera mozungulira cha ku Charlestown, kuyesetsa kuti ndipeze chinachake. Ambuye, zimawoneka ngati, amafuna kuti andiwuze chinachake, koma ine... Satana amayesetsa kuti ayime mnjira yanga, kundiletsa ine kuti ndisachite zimenezo. Chotero ine ndinaganiza, “Chabwino, ngati iye angachite zimenezo, ine ndingokhala ndikumadikirirabe, kumangodikirabe basi, kumangogogoda pa chitseko mpaka Iye atasegula.” Chotero ndiye mphindi zingapo zapitazo, kapena pafupifupi itangodutsa seveni koloko mmawa uno, ine ndinali nditadzuka molawirira kwenikweni.

<sup>15</sup> Dzulo, ndinadwala pang’ono, ndikuyesetsa... Ndinali nditadya chimanga chimene sindinagwirizane nacho bwino, pokhala kuti kunatentha kwenikweni, ndi ine—ine ndimayesetsa kuti ndichoke kwa izo. Ndipo—ndiyeno mmawa uno, pafupifupi eyiti koloko, ine ndinapezeka kuti ndinatenga Lemba limene linandidabwitsa ine. Ndipo ndinadzayang’ana pa Lemba limenelo kachiwiri, ndipo kachiwiri Ilo linandidabwitsa ine. Ndipo ndinapita, ndikulitsatira Ilo kudutsa mu Lemba, ndipo ine ndangotsiriza kumene maminiti pang’ono apitawo. Chotero izo mwinamwake zikhoza kukhala kuti Ambuye ali ndi Uthenga wa ife, mmawa uno, umene Satana wayesetsa kuwutchingira kwa ife.

Kodi mungamubweretse wamng’ono kuno, Mlango Larson? [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Mulungu akhale nawo ndi kuwathandiza iwo.

<sup>16</sup> Tsopano ndakhala ndikukusungani inu, Lamlungu lathali, masiku awiri, ndipo ine ndikuganiza... kapena, misonkhano iwiri, m’mawa ndi madzulo, ndipo izo zimapanga izo kukhala zovuta kwa inu. Ine ndamva kuti izo... Ena a inu mukuyenera kuti mupite kutali kwambiri, ndi kuphonya ntchito ya tsiku limodzi, ndi zina zotero. Chotero ngakhale ife tikuchoka Lamlungu, Lolemba, sabata, ine ndingolengeza msonkhano wa Lamlungu likudzali, Ambuye akalola, mwaona, pokhapokha ngati osonkhana angafune kuti iwo ukhale kuhezera usikuwu. Mwaona, izo, izo ziri... Pali ambiri a inu!

Ndi angati angakonde kuti izo zikhale usikuuno, tiyeni tiwone, tikhale ndi misonkhano usikuuno? Tsopano, amene angakonde kudzakhala nawo Lamlungu likudzali, kwezani dzanja lanu lotsatira? Ooh! Mai, izo zayandikana. Uh! [Wina akuti, “Zafanana, m’bale!”—Mkonzi]. Mukuti chiyani? [“Mudzakhala nawo nthawi ziwiri zonse.”] Uh! [M’bale Ben Bryant akuti, “Tikhale nawo usikuuno, ndi sabata yamawa, aponso, M’bale.”] Tsopano, tsopano, Ben!

<sup>17</sup> Ine ndiri ndi Uthenga uwu, ndi wautali, mmawa uno, koma ine—ine sindikudziwa momwe... Ndipo ine ndikudziwa ndimathandizira kupanga malamulo a mpingo, koma mmenemo,

ngati inu mungazindikire, ine ndinati, “Pokhapokha ngati ndikujambula.” Mukuona? Kotero, apa ndi ndikujambula. Uhuh. Chotero mwinamwake ife tiyesetsa kubwereranso nthawi ziwiri zonsezo, usikuuno ndi Lamlungu likudzali, ndiye, titero ngati Ambuye alola, inu mwaona. Tsopano, ngati inu simukhala ndi uthenga sabata ino, ndiye mudzabwere Lamlungu likudzali.

<sup>18</sup> Ndikudana nazo kuti mubwere kawiri monga choncho, koma ine ndikumverera kuti tiribe nthawi yochulukirapo. Ndipo mungokumbukira, ngati nthawi ipita patsogolo, sitidzakhala ndi mwayi uwu motalika kwambiri. Mukuona? Kumbukirani, chinachake chidzachitika. Mwina lamulo lidzatiletsa ife, kapena Satana adzasuntha pakati panu ndipo adzakubalalitsani inu. Izo nthawizonse zakhala ziri mwanjira imeneyo. Mukuona? Chinachake chidzachitika, chotero tiyeni tiziyamikira miniti iliyonse imene tikukhala tiri limodzi.

<sup>19</sup> Chotero tsopano kwa iwo amene akuyenera kubwerera kunyumba kwanu, usikuuno, zikhala ngati Lamlungu lapitali usiku, ine ndinangokhala ndi—a Uthenga waufupi wawung’ono. Ndipo kotero, inu, ngati inu mukuwufuna iwo pa tepi, bwanji, ife ndithudi tidzakutumizirani inu tepiyo ngati inu mukuyenera kubwerera kwanu. Ife sitiri. . . Ine ndilalikira usikuuno, ngati Ambuye alola.

<sup>20</sup> Ndinali ndi cholemba dzulo, kapena—kapena dzana, Uthenga wawung’ono umene ine ndinalimba kuchokera mu kukumbukira chinachake, ndipo iwo ndi wakale. Pali Mauthenga awiri, ngakhale. Ziri ngati pakati, umodzi wa iwo ndi, “Chitsime chowukha,” kapena, “Kufesa kwa mphepo ndi kututa kamvulumvulu,” basi Uthenga wa Ulaliki. Mmawa uno ndi kuphunzitsa. Ndipo kotero, usikuuno, ine mwina ndiyankhula pa, “Kufesa kwa mphepo ndi kukolola kamvulumvulu,” kapena, “Chitsime chimene chikuwukha.”

<sup>21</sup> Ndipo, mmawa uno, ine ndikufuna kuti ndiwerenge kuchokera mu Malemba Opatulika tsopano.

Ndipo kodi inu ndi omasuka? Nenani, “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Chabwino.

Tsopano ine ndikufuna inu, mu Mabaibulo anu, kuti mutsegule ndi ine ku Bukhu la Hoseya, inu amene mukufuna kuti muwerenge. Ndipo tiyeni tiwerenge ndime zingapo za mutu wa 6 wa Bukhu la Hoseya, mneneri.

Ndipo tiyeni tiyime.

<sup>22</sup> Wokonedwa Mulungu, ndife osayenera kutenga Bukhu ili mmanja mwathu, pakuti timawerenga m’Malemba kuti palibe munthu Kumwamba kapena pa dziko lapansi, kapena panso pa dziko lapansi, anali woyenera kapena ngakhale wokhoza kulitenga Bukhu, kapena ngakhale kuyang’ana pa Ilo. Oh, ndipo pamenepo panabwera Mmodzi yemwe anali ngati mwanawankhosa wophedwa; Iye anatenga Bukhu, pakuti Iye

anali woyenera, ndipo Iye anamasula Zisindikizo zake. Ndipo ife tikuyang'ana kwa Iye mmawa uno kuti awulule nkhani izi zimene zalembedwa mu Bukhu, chifukwa ilo ndi Bukhu la Chiwombolo. Onse amene anawomboledwa analembedwa mmenemo. Mulole ife tipeze malo athu, mmawa uno, mu nthawi imene ife tikukhalamo. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amenii.

*Bwerani tsopano, ndipo tiyeni tibwerere kwa AMBUYE: pakuti iye wang'amba, ndipo adzatichiritsa ife; iye wakantha, ndipo adzatimanga ife.*

*Akadzatha masiku awiri iye adzatilandira ife: mu tsiku lachitatu iye adzatiwukitsa ife, ndipo tidzakhala pamaso pake.*

*Pamenepo ife tidzadziwa, ngati tidzatsatirabe kumudziwa AMBUYE: kupita kwake kunakonzekereredwa ngati mmawa; ndipo iye adzabwera kwa ife ngati ka mvula, monga mvula ya masika ndi yanyundo pa dziko lapansi.*

*O Efraimu, ndidzakuchitira chiyani iwe? O Yuda, ndidzakuchitira chiyani iwe? pakuti ubwino wako uli ngati mtambo wa m'mawa, ndi ngati mame umachokapo.*

*Chomwecho ine ndawadula iwo mwa aneneri; Ine ndawapha iwo ndi mawu a pakamwa panga: ndipo ziweruzo zanu ziri ngati kuwunika kumene kumatulukira.*

*Pakuti ndinafuna chifundo, ndipo osati nsembe; ndi chidziwitso cha Mulungu koposa nsembe zopsyereza.*

*Koma iwo monga anthu alakwira pangano: iwo a—iwo andichitira ine zachiwembu.*

*Gileadi ndi mzinda wa iwo akuchita mphulupulu, ndipo wayipitsidwa ndi magazi.*

*Ndipo monga magulu a achifwamba adikirira munthu, momwemonso gulu la ansembe limapha mu njira mwa chilolezo: ndi . . . kuchita chidetso.*

*Ndawona chinthu choyipa m'nyumba ya Israeli: uko kuli uhule wa Efraimu, Israeli wayipitsidwa.*

*Ndiponso, O Yuda, iye watumiza zokolola kwa iwe, pamene ine ndinabweza amndende a anthu anga.*

<sup>23</sup> Ambuye Yesu, mutenge kuchokera Apa, mwa Mzimu Wanu Woyera, nkhani yomwe ikuganiziridwa, pamene ife tikuyembekezera mopitirira pa Inu. Mu Dzina la Yesu. Amenii.

<sup>24</sup> Tsopano, phunziro langa mmawa uno ndi: *Kulizindikira Tsiku Lanu Ndi Uthenga Wake.*

Ife tikuwona kuchokera mu phunziro la Lamlungu lapitali, monga ife tinaphunzitsira, *Phwando La Malipenga*. Ndipo ine ndikufuna kuti ndiyitanire tcheru chanu, tsopano, nthawi—nthawi ya Israeli mu nthawi ya Mulungu.

<sup>25</sup> Ife tikuchita lero pa phunziro la Sande sukulu, limene ine ndikufuna kuti inu muwone ndi kuzindikira nthawi imene ife tikukhalamo. Tatsala pang'ono kuti nthawi itithere, monga inu mukuwonera. Ndiyeno, mwa ichi, inu mukuyenera kudziwa ora lomwelo ndi nthawi, ndi chizindikiro ndi Uthenga umene inu mukuyenera kuwulandira.

<sup>26</sup> Tsopano, monga ife tinayambira Lamlungu lathali. . .Ife takhala tikuyankhula za kupita kukalalikira pa Malipenga, Malipenga Asanu Ndi Awiri otsiriza a Baibulo. Ndipo ine, mwa inemwini, ine ndimaganzira iwo akanatulukira chimodzimidzi monga ngati Zisindikizo. Koma ine ndazindikira kuti pa kutseguka kulikonse uku pakhala pali chinthu chachikulu chimene chimachitika.

Ndipo pamene tinkalalikira *Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo*, ndipo iyo inali mwangwiro kwambiri mpaka Mzimu Woyera Mwiniwake unadzabwera pansu pakati pathu ndi kudzatsimikizira izo, ndi kudzaziyika izo pa mapepala, ndi kudzaziponyera izo kudutsa fuko, ndi kudzaziwonetsa izo mu mwezi mmiyamba, ndipo anatsimikizira izo kwa ife, masabata ndi miyezi izo zisanachitike, kuti basi momwe izo zikanati zidzakhalire, mwangwiro. Kuno mu kachisi Iye anazidziwitsa izo. Kuno pa . . . mu nthawi, Iye anazidziwitsa izo. Pa mwezi ndi dzuwa, Iye anazidziwitsa izo. Ndipo m'malo a mafuko pa nthawi iyi, Iye anazidziwitsa izo; pamene ufumu wolowezana wa Roma ananyamuka ndi kubwerera ku Palestine, akuyenera kukhala papa woyamba kuyambira (iwo amatero) Petro kukhala papa. Tsopano, izo zinali zopambana kwambiri!

<sup>27</sup> Ndiye, ife tikuona, zisanachitike Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri zomwe zinabisa zinsinsi zonse.

Ine osadziwa chimene ndinkajambula pa bolodi, kwa Mibadwo ya Mpingo. Ine sindinatero. Mulungu akudziwa. Mwa masomphenya basi, ine ndinajambula izo. Osadziwa kuti Mulungu, pakadzatha chaka ndi miyezi sikisi, adzatsimikizira icho mu mlengalenga, pogwiritsa ntchito mwezi, ndi kudzazilemba izo pamapepala a dziko lonse. Ine sindimadziwa zimenezo. Ine sindimadziwa kuti pakanadzakhala mdima wachinsinsi mu mwezi, wodzaimira M'badwo wa Laodikaya uno.

<sup>28</sup> Tsopano, pa mapepala, inu munangopeza mibadwo sikisi yokha. Ndi chifukwa chakuti mpingo wa Laodikaya unadetsedwa kwathunthu. Ndipo ngati inu mungazindikire kamvetsedwe kauzimu, monga Mulungu anaziyikira izo kumwamba. Pamene ine ndinayika izo pano pa dziko lapansi,

ine ndinasiya ka danga kakang'ono, monga inu mukuwonera, kuwala pang'ono chabe. Izo zinali basi Osankhidwa omwe asanayitanidwe kuchokera pa dziko lapansi, chifukwa chimene ine ndinayikira izo pamenepo kwa m'badwo wachisanu ndi chiwiri. Koma pamene Mulungu anadzayika izo mmiyamba, izo zinadetsedwa kotheratu, zikutanthauza kuti mwinamwake wotsirizayo akuyitanidwa kuchokera ku M'badwo wa Laodikaya umenewo. Ife sitikudziwa. Pakhoza kukhala ulaliki pa zimenezo.

<sup>29</sup> Tsopano zindikirani kachiwiri, zisanafike a—Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwi, zomwe ine sindimadziwa kuti izo zinali mwanjira imeneyo.

Kuno ku kachisi Iye anadzayankhula za zimenezo, ndipo ananditumiza ine ku Tucson, Arizona, kudzakuzani inu nonse zomwe zikanati zidzachitike. Ndipo pali amuna amene alipo, lero, amene anali kumeneko kuti adzawone izo zikuchitika basi ndendende momwe izo zinanenedwera kuno kuti zikanadzachitikira, “Angelo asanu ndi awiri akanadzabwera.” Kenako manyuzipepala analemba izo, ndi magazini, kudutsa fukoli, “Mkombero wodabwitsa wa Kuwala mmawonekedwe a piramidi,” chimodzimodzi basi monga momwe ndinajambulira izo kuno ndi kukuwonetsani inu. Unakwera mmwamba kuchokera pamene Angelo amenewo anayima, ndipo unapita mailosi sarte kutalika, ndipo unali mailosi twente-seveni chopingasa; kapena mailosi twente-seveni kutalika, ndi mailosi sarte chopingasa, ine ndayiwa chomwe icho chinali. Ndipo unawoneka mmadera onse, kumtunda kwa Tucson, Arizona, komweko kumene izo zinachitikira, nthawi yomweyo.

<sup>30</sup> Mwaona, a—Baibulo, Mulungu si basi. . . Uyu si winawake kuti akuyesera kuti—akanikizire chinachake kwa inu, koma kuti awululire kwa inu kumvetsa kumene kwauzimu kwa ora lino.

<sup>31</sup> Ndipo kenako, Uthenga wotsatira, umene unadzatsigula Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwi, umene unamasula zinsinsi zonse zobisika za Baibulo, Ziphunzitsa, ndi zina zotero. Chimene, dziko mwamwano kwambiri limaukura masiku ano, likuwukira Ilo ndi kunena kuti Ilo ndi lolakwika, *ichi, icho*.

<sup>32</sup> Kuno tsiku lina mu Arizona, akulumikiza matepi, akuyesetsa kuti andipangitse ine kunena zinthu zomwe sindinanene. Mungokumbukira masomphenya a malingaliro aku Arizona! Baibulo linati, “Zikanakhala bwino ngati inu mukanakhala ndi thanthwe litamangiridwa pakhosi panu.” Ndipo chinthu china, nchakuti, “Aliyenseyo,” kaya ndi mlaliki kapena chimene iye angakhale, “akadzachotsa Mawu amodzi kwa Ilo, kapena kuwonjezera mawu amodzi kwa Ilo!” Anthu kumayika kutanthauzira kwawo kwawo pa Mawu monga Iwo aperekedwera, kuyesetsa kuwapangitsa Iwo kunena chinachake chimene ine sindinanene, ndipo, si Mawu anga; Iwo ndi Mawu Ake. “Amene adzawonjezera, kapena kuchotsapo!”



<sup>33</sup> Ndipo kenako, mmasomphenya, ife tinawawona aneneri awa akubwera mwakamvuluvulu, monga ine ndinafotokozera kwa inu, ine ndikukhulupirira, ma Lamlungu angapo apitawo. Zonse zidzakhala. Ine ndinati, “Mungokhala kutali kwa izo.” Bola ngati ine ndikumenyana nazo, ndiye kuti Mulungu sangamenyane nazo. Koma tiyeni timulole Iye akhale nazo izo. Iye ndi Mmodzi Amene amasamalira izo. Mukuona?

<sup>34</sup> Tsopano ife tinazindikira, Lamlungu lathali, uko kunali . . . ndimalalikira masiku aphwando. Ndipo panali phwando la pentekoste. Ndipo pakati pa phwando la pentekoste ndi phwando la malipenga, iyo inali nthawi yayitali; ndendende masiku fifite pakati pa pentekoste ndi phwando la malipenga. Ndipo masiku fifite, omwe, *pentekoste* imatanthauza “fifite.” Kunali kuweyula-ntolo, kapena ingat- . . . Zipatso zoyamba za zokolola zinabweretsedwamo. Ndipo ife tikuwona izo zinali mu choyimira kumbuyo uko, ndi zipatso zoyamba zachirengedwe, kuimira zipatso zoyamba za Mzimu Woyera kuti zitsanuliridwe pa anthu.

Ndipo ife tikupeza, ndiye, kuti masiku fifite amenewo analandiridwa ndi Amitundu, zomwe, “Mulungu anayitana kuchokera kwa Amitundu anthu a Dzina Lake,” phwando la pentekoste. Ndipo ife takhala tikudutsa mu phwando la pentekoste lalitali limenelo.

<sup>35</sup> Tsopano, kwenikweni, kuchokera ku masiku fifite, angakhale ndendende masabata seveni. Ndipo masabata seveni ankaimira Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo, yoti idzaitanidwe mu nthawi ya phwando la chipentekoste, la Pentekoste, kudzaitana anthu kuchokera kwa Amitundu chifukwa cha Dzina Lake.

Tsopano, pa mapeto a masabata seveni awa, amene akhala ali, pankayenera kukhala Tsiku la Chitetezero, limene linali Malipenga Asanu Ndi Awiri. Ndipo Malipenga Asanu Ndi Awiri anali oti adzaitane tsiku la kulira, kubwerera ku Nsembe, kapena, Chitetezero. Ndipo ife tikupeza ndiye, kuti, Israeli, Malipenga Asanu Ndi Awiri ankakhudza Israeli yekha.

<sup>36</sup> Ndipo, ndiye, chifukwa chimene Iye sanandirole ine kuti ndilalikire Malipenga Asanu Ndi Awiri amenewo. Ine mpaka ndinali nditakonzeka kuti ndilengeze zimenezu, ndinali nditakonzeka maholo ndi chirichonse choti ndilowemo, kuti ndidzalalikire Malipenga Asanu Ndi Awiri. Ndipo ine ndinati, “Pali chinachake chimene chikundivutitsa ine kwambiri,” Ine ndinatero. Ife tinakhala tikugwirabe ntchito, ndipo Billy ndi tonse a ife, kuyesetsa kuti tikonze chirichonse chokonzekera zoziziritsira mchipinda, kwa sabata ikubwerayi, kwa Malipenga Asanu Ndi Awiri; kukhala ndi masiku teni, kapena masiku eyitu, tinali ndi holo ya sukulu. Koma Mzimu Woyera sunandilole ine

kuti ndichite izo, pa chifukwa china, ndipo ine ndimadabwa kuti bwanji.

Ndipo pamene ine ndinapita kuti ndikapemphere, ine ndinamuza mkazi wanga, “Ine ndikukalowa.” Ndipo moonamtima ndinagwada pansi pamaso pa Mulungu, kuti ndipemphere. Ndipo Iye anawulula kwa ine kuti Malipenga Asanu Ndi Awiri amenewo anawomba pansi pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi, ndipo ndinali nditalalikira kale izo, mwauzimu. Mwaona, ndi dzanja la Mulungu, chinthu chonsecho. Izo ndi zokhudzana ndi Israeli, ndipo ife tinazitenga izo mu Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi; inu nonse amene muli nazo izo, momwe zinakhallira ndi mazunzo a Ayuda.

<sup>37</sup> Nthawi ya Amitundu yakhala ili mu phwando la chipentekoste ili.

Malipenga, pansi...zonsezo zinawombodwa pansi pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi. Ndipo ife tinazitenga izo Lamlungu lathali, pansi pa phwando la Malipenga, ngati inu nonse mukufuna kuti mupeze izo. Kodi izo zinali zoti zidzachite chiyani? Kudzawathamangitsira Ayuda, kuchokera ku madera onse a dziko, kubwerera ku dziko la kwawo. Izo zikuyenera kukhala pamenepo. Ndi kutsegula kwa Zisindikizo, pansi pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi, ndi pansi... Malipenga Asanu Ndi Awiri anawomba mu—Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi.

<sup>38</sup> Tsopano, Uthenga wa mngelo wachisanu ndi chiwiri ndi woti udzatsegule chinsinsi cha Zisindikizo, kuyitanira antchito Amitundu a ora la chileveni kuti adzalandire malipiro omwewo amene ogwira ntchito a ora loyamba analandira. Mukuona?

Tsopano, Yesu anaphunzitsa izo. Iye anati panali anthu ena amene anapita kukakolola. Iwo analembodwa ganyu. Ndipo pamene iwo anatero, m’bandakucha, iwo analandira a—a—a nthawi, khobiri la tsiku. Ndipo kenako masana, winawake anadzabwera ndipo anapita kukagwira ntchito. Ndipo kenako pa ora la chileveni, ndiro ora lomaliza la tsiku, kuti wina anadzabwera ndipo anadzalandira malipiro ofanana ndi omwe iwo anachita pa ora loyamba la tsiku; ora lomaliza.

<sup>39</sup> Izo ndi zangwiro kwambiri, momwe atumiki a ora loyamba ali ndi Mawu, ali ndi Uthenga, ali ndi Choonadi, iwo anabwera mmenemo pa Tsiku la Pentekoste. Kenako panadzabwera m’badwo wa mdima umene unadzawatserekerezera iwo panja. Kenako pakati pa tsiku, Luther, ndi Wesley, ndi iwo, anadzabweramo. Ndipo kenako pakuyenera kudzakhala Uthenga wa nthawi ya kumadzulo, ndi kudzalandira chinthu chomwecho chimene iwo anachita pachiyambi. Uthenga wa nthawi ya kumadzulo ndi woti udzabwezeretsenso kachiwiri, kudzabwezeretsanso chinthu chomwecho kachiwiri.

<sup>40</sup> Ndipo mukukumbukira masomphenya a sabata yatha, kuti pamene Mkwatibwi anadzabwera kuti adzakhale... chiwonetsero cha izo. Apo panabwera Mkwatibwi wamng'ono, wokonedwa, mmasomphenya. Ndipo ine, ndisakuganizira za izo; nditangokhala pamenepo ndikuyang'ana panja. Ndipo apo panadzabwera Mkwatibwi. Ine ndinamva Liwu pambali pa ine, linati, "Ichi ndi chiwonetsero cha Mkwatibwi." Ndipo Iye anabwera pafupi. Ine ndinamuzindikira Iye, momwe Iye analiri, wokonedwa kwambiri, wokongola, wamng'ono. Iye anali akuyenda sitepe basi momwe Iye akanathera, osati kuguba; basi mu kayendedwe ka a—mkazi, momwe iwo amayendera mwachisomo, ngati dona. Umo ndi momwe Iye ankayendera, akubwera kumanzere kwanga mbali *iyi*, ndipo Iye anadzachoka sindimamuwonanso.

<sup>41</sup> Kenako Iye ananditembenuzira ine ku mbali yakumanja, ndipo Iye anadzandiwonetsa ine mpingo uliwonse momwe iyo yakhala ikubwerera kuchokera mmibadwo. Ndipo, oh, zonyansa bwanji! Ndipo wotsiriza unali m'badwo uwu wa mpingo wa tsiku lotsiriza, umene unkatsoledwa ndi mfiti. Ndipo iwo anali atavala mopanda makhalidwe kwambiri, owoneka-monyansa kwambiri! Ndipo iwo anali akuguba mwa kuzithyola kwa nthawi ndi gwedemula. Ndipo akazi amenewo akungodziponya okha mu kuzithyolako, atangonyamula kapepala, kotuwa, chinyengo, a... Kutuwa kumakhala pakati pa choyera ndi chakuda, womwe ndi mtundu wonyenga. Kutuwa si choyera kapena chakuda. Ndi mtundu wonyenga. Ndi pepala lowoneka lotuwa, atalinyamula kutsogolo kwawo, ndi masiketi owoneka ngati azingwe ali kutsogolo kwawo, ndipo amaliseche kwathunthu kuyambira mchiuno mwawo kumakwera mmwamba. Ndipo anali akuguba waku... kapena nthawi, kapena akuzithyola, ndi kumapitirirabe ndi nyimbo imeneyo, ndi kumayenda chokwezeka. Ndipo anati, "Umenewo ndi mpingo."

<sup>42</sup> Ndipo pamene iwo unadzandidutsa ine, mtima wanga unakhala ngati ukomoke. Ine ndinaganiza, "Ngati icho ndi chimene chikuyesera kuti chiperekedwe kwa Khristu, ngati Mkwatibwi? Mwa kuyesetsa konse ndi zinthu zomwe munthu waziyika, kuyesetsa kuti abweretse Mkwatibwi kwa Khristu; ndipo wachiwerewere wanyansi, wosasamba, wowoneka-mwauve monga ameneyo kukhala Mkwatibwi wa Khristu?" Izo zinandidwalitsa mumtima mwanga.

<sup>43</sup> Ndipo pamene iye anali kudutsa, iye ata... Akubwera pomwe ife tinali titayima, iye anali atanyamula pepala kutsogolo kwake, akuzithyola, ndi kumazigwedemula, ndi kumadzisunthira yekha mbali imodzi ndipo kenako mbali inayo, pamene anali kupita, monga kuvina kwamakono komwe iwo ali nako kwa tsiku lino, akudzigwiritsa ntchito yekha mu mchitidwe achiwerewere pamene iye anali kuguba chitsogolo.

<sup>44</sup> Ine sindikuyankhira pa zinthu izi. Ine ndikhoza kungonena zomwe ndinaziwona. Ndipo Mulungu monga Woweruza wanga, koma umenewo unali mpingo wochokera ku U.S.A.

<sup>45</sup> Tsopano, pamene iye amadutsa, mbali yonse ya kunsana inalibe chophimba nkomwe. Ndipo kenako pamene iye amadutsa, ine ndinamverera kukomoka ndi kudwala.

<sup>46</sup> Kenako Iye anati, “Mkwatibwi adzawonekeranso kachiwiri.” Ndipo apa Mkwatibwi anabwera mmbuyo mwa iye, Mkwatibwi wowoneka-momwemo yemwe anadutsa poyambirira. Zitatero mtima wanga unalumpha ndi chimwemwe, kudziwa kuti padzakhala Mkwatibwi. Ndipo Iye adzapangidwa kuchokera ku chinthu chomwecho, ndipo adzavekedwa mu chinthu chomwecho, chimene Mmodziyo anali pachiyambi. Iye ndi woti adzaitanidwa.

Ndipo ine ndikudziwa kuti icho ndi Choonadi. Ngati izo si zoonza, ndiye kuti masomphenya aliwonse amene ine ndakhala ndiri nawo mmbuyomu akhala ali olakwika. Ndipo aliyense akudziwa, kuti, palibe chinthu chimodzi chimene Iye anayamba watiuzapo ife koma chimene chinali Choonadi. Ichu chinadzafika pochitika, basi. . .

<sup>47</sup> Ndipo kodi inu mukuwona, ndiye, nyansi za mpingo wamakono, ukudzitcha wokha “mpingo”?

<sup>48</sup> Monga wina ananenera tsiku lina; M’bale Ruddell, m’bale wanga wofunika, wayima motsamira khoma apo tsopano. Kutu, iye anaziwona izo ngati nthambi pa mpesa. Ndipo ife tinali kukambirana izo mu chipinda tsiku lina. Ndipo M’bale Ruddell anasokonezeka ndi zochitika za nthawiyi ndi—ndi kumverera kwa mzimu mmipingo lero, momwe zayambira kutsika pansu. Atumiki kumabwera kuchokera konsekonse, ndi zoyankhulana zapadera kunja kuno, kumafunsa, “Chachitika ndi chiyani, M’bale Branham? Chachitika ndi chiyani?” Oh, mai!

<sup>49</sup> M’bale Ruddell anandifunsa ine funso, “Kodi iwo akukhala moyo ndi mzimu wa Satana, kapena chiyani?”

<sup>50</sup> Ine ndinati, “Ayi, nthambiyu imakhala moyo ndi mphamvu ya mpesa.” Iyo imakhala moyo chifukwa, chipatso chowawasacho, a—mandimu amamera mu mtengo wa lalanje; koma iwo sumabereka malalanje, ngakhale ukukhala ndi moyo chifukwa cha iwo.

Ndipo mpingo, wotchedwa, wangokhala nthambi yomezanitsidwa, ukukhala moyo pansu pa dzina la chipembedzo, pansu pa dzina la mpingo. Akatolika ndi Achiprotectanti, nthambi chabe, akukoka a . . . kuchokera ku mphamvu ya Mpesa; ndipo komabe kumabala chipatso cha chimene iwo ali, chifukwa iwo sanatembenuke. Iwo sanali mu dongosolo lapachiyambi, lokonzedweratu la Mulungu, ndi chifukwa chake iwo amayenera kuti awakane Mawu ndi kumabala mtundu wina wa chipatso. Mtengo weniweni wapachiyambi, mu muzu

wake, unakonzedweratu kuti udzabale malalanje pa mtengo wa lalanje.

Yesu anati, “Ine ndine Mpesa; inu ndinu nthambi.”

<sup>51</sup> Koma ngati mtengo umenewo udzatulutsa konse nthambi ina, iwo udzabala chipatso chake chapachiyambi. Ndipo pakuyenera kukhala kubwezeretsedwa kwa zinthu zonsezi, pa mapeto pomwe pa Mpesa. Pakuyenera kukhala, kubwera, kubwezeretsa, Kuwala kwa kumadzulo kuti kudzawalitse Iwo ndi kudzawukonza Iwo. Koma izo zidzabwera kuchokera mu Mpesa, osati chipembedzo chimene chamezetsanidwa mwa Iwo; koma kupukusa kwapachiyambi kwa Mawu. Iwo akuyenera kubwera ku nthawi ya kumadzulo. “Ndipo padzakhala Kuwala mu nthawi ya kumadzulo.” Zimatengera Kuwala kuti kukhwimitse Iwo.

<sup>52</sup> Mwaona momwe Malemba aliri angwiwo! “Tsiku lomwe silidzatchedwa masana kapena usiku.” Chipatso sichingache pokhapokha dzuwa litachetsa icho. Ziribe kanthu ndi mochulukha bwanji momwe inu mungalalikire, chirichonse chimene inu mungachite, icho sichingakhoze kucha, icho sichingawonetseredwe, icho sichingatsimikiziridwe; kokha ndi Iye Amene anati, “Ine ndine Kuwala kwa dziko lapansi,” Mawu. Chotero pakuyenera kubwera a—a—a Mphamvu, Mzimu Woyera Mwiniwake, kuti udzachetse, kapena kutsimikizira, kapena kudzatsimikizira, kapena kudzawonetsera icho chimene Iye ananeneratu kuti chikanadzachitika mu tsiku lino. Kuwala kwa kumadzulo kukupanga zimenezo. Ndi nthawi yotani!

<sup>53</sup> Mkwatibwi anadutsa malo omwewo amene Iye anali pamene Iye anali pachiyambi. Koma ndinali kumuwona Iye akuchoka pa sitepe, ndi kumayesera kumukokera Iye mmbuyo. Tsopano, zambiri zikhoza kunenedwa pa zinthu izi, za tsiku lomwe ife tikukhalamo.

<sup>54</sup> Tsopano, Hoseya anati, mu 6:1, “Bwererani kwa Ambuye.” Kumbukirani, iye ananena kuti iwo adzabalalitsidwa, ndipo iwo anatero. Iye anati, “Iwo adzabwerera kwa Ambuye, iwo atabalalitsidwa, ndipo Iye adzatero, adzawamanga iwo.” Zindikirani, “Bwererani...Adzabalalitsidwa; chachiwiri... Iwo anang’ambidwa, ndipo anachititsidwa khungu.” Ndizo ndendende zomwe zinachitika. “Iye adzatichiritsa ife, ndipo adzatimanga ife.”

Monga Ezekieli 37, “Mafupa owuma, chigwa chodzaza ndi mafupa owuma.” Ezekieli anachiwona icho, kubwerera kwawo kachiwiri.

Ndiye zindikirani, Hoseya anati, “Akadzatha masiku awiri!” Akadzatha masiku awiri Iye adzabwerera kwa iwo. “Iye adzatilandira ife ndipo adzatipatsa ife, adzatitsitsimutsa ife.” Tsopano, *kutsitsimutsa* sikutanthauza “chiwukitsiro.” *Kutsitsimutsa*, apo, ndi mawu omwewo amene amagwiritsidwa

ntchito kwina kulikonse, ine ndinangowayang'ana iwo, amatanthauza, “chitsitsimutso.” “Iye adzatitsitsimutsa ife akadzatha masiku awiri.” Izo zidzakhala, “Patsiku lachitatu Iye adzatitsitsimutsanso ife, Iye atatibalalitsa ife, ndi kutichititsa khungu, ndi kuting'amba ife.”

<sup>55</sup> Inu mukudziwa, Ayuda anachititsidwa khungu kwa cholinga chomwecho kuti ife tidzapenye. Iwo anang'ambidwa, ndi kumwazidwa, monga fuko, ndipo anamukana Mesiya wawo; kuti ife tidzakhoze kumulandira Mesiya, kuti padzakhale anthu oyitanidwa kuchokera mwa Amitundu chifukwa cha Dzina Lake.

<sup>56</sup> Tsopano, mwamuna amabwera, ndipo mkazi amadzatenga dzina lake. Amitundu ochititsidwa akhungu awa omwe sangathe kuliwona Dzinalo, “Ambuye Yesu Khristu,” mu ubatizo! Basi ndi zoyipa kwambiri, koma izo ziyenera kukhala mwanjira imeneyo. Ayuda, iwo ankayenera kutero—iwo ankayenera kuti asawone izo. Alipo mmodzi yekha amene angawone izo; ameneyo ndi amene anakonzedweratu kuti adzawone izo. Apo ayi, simudzaziwona izo konse.

Ayuda sakanatha kumuwona kuti anali Mesiya wawo. Ndipo, komabe, iwo anali masikolala ndi azaumulungu, amuna amaphunziro odziwika kwambiri, ankawerenga Baibulo lomwelo limene inu mumawerenga. Tsopano, izo zitadziwika kwa ife, ife tikhoza kuziwona izo momveka, ameneyo anali Mesiya. Koma, iwo sanathe kuziwona izo, komanso iwo sangathe kuziwona izo lero. Iwo analoseredwa kuti adzachititsidwa khungu, nawonso.

<sup>57</sup> Mpingo, lero, waloseredwa kuti ndi wakhungu, ukukana Uthenga wa nthawi ya kumadzulo. Chivumbulutso 3 ananena chomwecho, “Ndinu atsoka, omvetsa chisoni,” zindikirani khalidwe la mkwatibwi usiku wina, kapena mpingo, “wamaliseche, wakhungu, ndipo osadziwa izo.” Ambuye Yesu, tichitireni chifundo ife! Baibulo linati iye anali “wamaliseche.” Ine sindinaziwone izo mpaka pano. Mpingo wa Laodikaya unali wamaliseche. Ndipo pamene iye anawonekera usiku wina, iye anali “wamaliseche,” sindinazindikire izo, “ndipo sindimazidziwa izo.”

<sup>58</sup> Oh, ndikuthokoza bwanji! Motani, nzosadabwitsa kuti ife ndi oyamikira kwambiri! Ine ndikumverera kuti sitiri oyamikira mokwanira pa zinthu zimene Mulungu akutidziwitsa ife.

<sup>59</sup> “Wamaliseche.” Ndipo masomphenyawo anati, anandiwonetsa ine kuti iye anali wamaliseche ndipo samadziwa izo, ndi “wakhungu.” Monga Israeli anachititsidwa khungu kuti Amitundu alowemo, tsopano Amitundu achititsidwa khungu kuti Mkwatibwi akhoze kutulutsidwa ndipo Israeli akhoze kulandira phwando la Malipenga. Mwangwirowo basi!

<sup>60</sup> “Akadzadutsa masiku awiri Iye adzatitsitsimutsa ife, kapena adzatipatsa ife chitsitsimutso, kudzatisationkhanitsa ife pamodzi, Ayuda,” kuyankhula pa Malipenga awa tsopano. Ndipo Iye adza... “Ndipo ife tidzakhala moyo pamaso Pake, kapena tidzakhala ndi Moyo Wamuyaya. Mwaona, ife tidzakhala pamaso Pake.” Baibulo linanena apa mu Hoseya, linati, “Ndipo ife tidzakhala pamaso Pake; Moyo, tidzakhala ndi Moyo pamaso Pake.” Umenewo ndi Moyo Wake Womwe, Moyo Wamuyaya, “tidzakhala ndi Moyo pamaso Pake.”

“Iye amene amakhala mu zosangalatsa ndi wakufa pamene iye ali ndi moyo.” Chotero ife... analonjeza kuti Israeli kachiwiri adzakhala ndi Moyo pamaso Pake. Iye wakhala wakufa, ku zowona, ndi ku phwando la pentekoste.

<sup>61</sup> Tsopano zindikirani, mosamalitsa. “Ndiye akadzatha masiku awiri.” Tsopano, izo sizimatanthauza masiku awiri a maora twente-foro, chifukwa pakhalala pali... Zimenezo zinachitika mmbuyo kale, zaka mahandirede ambiri zapitazo. Mukuona? Izo zimatanthauza, “masiku awiri ndi Ambuye,” zikadzatha zaka thuu sauzande. Tsopano, inu mukudziwa kuti zakhala nthawi yayitali bwanji kuyambira nthawi imeneyo? Zakhala ziri zaka twente-seveni handirede kuchokera pamene, chifukwa mu Hoseya apa ndi B.C. 780. 1964, mwaona, zakhala ziri chinachake kupitirira zaka twente-seveni handirede zapitazo. Iye anati, “Akadzatha masiku awiri, mu tsiku lachitatu, Iye adzatitsitsimutsanso ife, ndipo adzatipatsa ife Moyo pamaso Pake.” Ndi amenewo Malipenga anu akubwera. Ndiro ora limene ife tikukhalamo, tsiku limene ife tikukhalamo.

<sup>62</sup> Tsopano, iwo amwazikana, achititsidwa khungu, asonkhanitsidwa, ndipo ali patali mu tsiku lachitatu. Inu mukuona zimenezo? Iwo anamwazikana, kuchokera ku Palestina, kudutsa mdziko lonse. Iwo anachititsidwa khungu, kuti amukane Mesiya. Ndipo tsopano iwo asonkhanitsidwa mdziko lawo, akukonzekera Malipenga, kuti adzachizindikire Chitetezero.

Monga Baibulo linanenera, “Pamene iwo adzalandira Icho, ndi kudzamupeza Iye ali ndi zipsyera za msomali,” Mpingo utatengedwa, “ndipo iwo adzati, ‘Inu munazitenga kuti zipsyera izi?’ Iye anati, ‘M’nyumba ya abwenzi Anga.’” Ndipo Iye anati, “Iwo adzazipatula, banja lirilonse, ndipo adzalira ndi kuisisima, kwa masiku, ngati banja limene linataya mwana wawo wamwamuna mmodzi yekhayo.” Kumbukirani, phwando lija la Malipenga linali loti lidzachite zimenezo. “Kudzalira, kubuma chifukwa cha Nsembe imene inaphedwa,” ndipo iwo anali atayikana Iyo.

<sup>63</sup> Iwo ali mdziko lawo. Iwo anamwazikana, anachititsidwa khungu, ndipo tsopano asonkhanitsidwa. Ndipo zonsezo zinali pansu pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi

chimenecho, Malipenga awo Asanu Ndi Awiri...anawomba kuti awasonkhanitse iwo pamodzi, Lipenga Lachisanu Ndi Chimodzi. Lachisanu Ndi Chiwiri ndi “Lipenga Lalikulu lija,” monga ife tinali nazo Lamlungu lapitali. Lipenga Lachisanu Ndi Chimodzi linawomba pansu pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi. Chimodzimodzi monga momwe Chisindikizo chatu Chachisanu Ndi Chimodzi chinatsegulidwa, chirichonse pa nthawi yomweyo; kokha, zawo zonse zinawomba kamodzi; kumene, ife takhala zaka thuu sauzande mu phwando la pentekoste.

<sup>64</sup> Tsopano, zaka twente-seveni handirede kuchokera nthawi imeneyo. Iye anati, “Mu tsiku lachitatu, tidzasonkhanitsidwanso. Akadzatha masiku awiri, mu tsiku lachitatu, ife tidzasonkhanitsidwa kachiwiri, ndipo tidzalandira Moyo pamaso Pake.” Kodi inu mukuliwona lonjezolo? Ora linalamba mwangwiro pa khoma. Ife tikuwona pamene ife tiri.

<sup>65</sup> Tsopano mdziko la kwawo, akuyembekezera Phwando la Malipenga, kapena kuzindikira kwa Chitetezero, ndi kuyembekezera Kudza, kuti adzalire chifukwa cha kukanidwa kwawo kwa nthawi yoyamba yomwe iwo anachikana Icho. Iwo ali mdziko la kwawo chifukwa cha zimenezo, akuyembekezera. Onsewo ndi chiyani... Chirichonse chayikidwa pamalo ake.

<sup>66</sup> Monga mtumiki wa Uthenga, ine sindingathe kuwona chinthu chimodzi chatsalira koma kupita kwa Mkwatibwi. Ndipo Mkwatibwi akuyenera kuchotsedwa iwo asanazindikire chomwe chinachitika. Iwo anamangidwa, anamwazikana... Ine ndikutanthauza, iwo anamwazikana, anachititsidwa khungu, ndipo tsopano asonkhanitsidwa. Chatsalira ndi chiyani? Mkwatibwi kuti achotsedwe panjirapo. Kuyembekezera kupita kwa Mkwatibwi, kuti aneneri awo a Chivumbulutso 11 akhoze kuwaitanira iwo ku phwando la Lipenga, kuti akawapangitse iwo kuzindikira chimene iwo achita.

<sup>67</sup> Kumbukirani, pakati pomwe pa Zisindikizo zimenezo, panadzabwera Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi. Ndipo panali handiredi ndi forte-foro sauzande, osankhidwa ndi oyitanidwa. Ndipo pakati pa Lipenga Lachisanu Ndi Chimodzi ndi Lachisanu Ndi Chiwiri, Chivumbulutso 11 akuwonekera apo pomwe ndendende mogwirizana ndi Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi.

<sup>68</sup> Kudzachita chiyani? Kodi icho chinali choti chidzachite chiyani? Ndipo uku kunali kutulutsa mboni ziwiri, Mose ndi Eliya, aneneri. Chimene, Ayuda amakhulupirira aneneri awo okha. Ndipo iwo adzabwera ndi chizindikiro cha aneneri, ndipo ntchito yawo idzakhala ya mneneri, pakuti iwo anachita ndendende.

Kuwonetsera chinthu chimodzi, kuti, munthu, pamene iwe umwalira kapena chirichonse, pamene uchoka mdziko lino,



chikhalidwe chako sichimasintha. Ngati uli wabodza tsopano, udzakakhala wabodza kumeneko. Ngati uli waukali kuno, udzakakhala wawukali kumeneko. Ngati uli wokaikira kuno, udzakakhala wokayikira kumeneko. Amuna ndi akazi, ndi nthawi yoti mudzigwedeze nokha ndi kudzifufuza nokha, ndi kuwona pamene ife tayima, pakuti imfa simasintha izo.

<sup>69</sup> Iwo anali atapita kwa zaka thuu sauzande. Mose kwa pafupifupi zaka twente-faivi handirede, ndi Eliya kwa nthawi zonse kuyambira... Pafupifupi zaka twente-faivi handirede Eliya anali atapita, ndipo Mose anali atapita, ndipo apa iwo abwerera ndi chikhalidwe chomwecho ndipo akuchita zinthu zomwezo.

Imfa siimachita kanthu kwa munthu koma kusintha malo ake okhala. Siimasintha chikhalidwe chako. Siimasintha chikhulupiriro chako. Siimasintha chirichonse mwa iwe koma malo ako okhala.

<sup>70</sup> Chotero, momwe chikhalidwe chako chiriri mmawa uno! Ngati ndiwe wokayikira Mawu a Mulungu, iwe ukakhala wokayikira kumeneko. Sindikusamala kuti ndiwe oyera bwanji, momwe umakhalira moyo, ndi momwe umakhalira bwino, izo sizingakusithe iwe mpang'ono ukafa, malo okhalako ako basi. Ndipo ngati sungawavomereze Mawu onse a Mulungu momwe Iwo analembedwera, iwe sungakachite izo Kumeneko; chotero, usadandaule, iwe sukakhalako Kumeneko.

Iweu ukuyenera kuwalandira Iwo mu chidzalo Chake, mu mphamvu ya kutsimikiziridwa Kwake ndi vumbulutso la chimene Iwo ali, zikatero udzakhala gawo la Iwo. Ndi Mawu Ake Okha amene Iye ati adzawadzutse, monga Iye anachitira Mawu Ake mmawa woyamba wa Isitara. Mawu Ake okha anatulukira, ndipo iwo amene anafa mu Mawu Ake, akukhulupirira Mawu Ake ndipo anatsimikizira Mawu Ake.

<sup>71</sup> Zindikirani, tsopano, zimenezo zakhala ziri zaka twente-seveni handirede zapitazo. Zindikirani, iwo anamwazikana, iwo anachititsidwa khungu, ndipo tsopano iwo asonkhanitsidwa. Tsopano, chinthu chotsatira ndi chakuti iwo ndi oti alandire Moyo.

<sup>72</sup> Ndipo Amitundu ayitanidwa. Mkwatibwi wakonzeka. Mkwatulo uli pafupi. Kodi tikukhoza kuzindikira zimenezo? Kodi ife tingakhulupirire izo kwenikweni? Kodi imeneyo ndi nkhani yomwe yanenedwa? Kodi ndi nthano, kwa ife? Kodi ndi chinachake chomwe chikumveka chenicheni? Kodi ndi chinachake chimene ife, kunja, tingakhulupirire? Kapena, kodi ndi chinachake chimene chiri mwa ife, chimene chiri gawo la ife, chimene chiri choposa moyo kwa ife? Kodi ife tikuyikamo kachitidwe kotani, mmawa uno, mu kachisi uyu? Kumbukirani, ilo lidzakhala gulu laling'ono lomwe lidzaulandire Iwo.

<sup>73</sup> Tsopano ali ku dziko lakwawo, akuyembekezera Malipenga. Tsopano akuyembekezera kupita kwa Mkwatibwi wamng'ono, kuti Chivumbulutso 11 akhoza kukwaniritsidwa. M'badwo wa mpingo watha; Zisindikizo zatsegulidwa, zomwe zikutsimikizira zomwe iwo anazisiya mu m'badwo wa mpingo, ndipo Uthenga waperekedwa. Israeli ali pamalopo, aléluya, wakonzekera Phwando la Malipenga.

<sup>74</sup> Oh, amuna inu mmayiko ena kumene inu mudzamve tepi iyi, kodi simungadzuke, m'bale wanga? Kapena, kodi Iwo akukuchititsani inu khungu? Kodi inu mungawataye Iwo ndi kuwutcha Iwo ulosi wabodza? Pamene, Iwo atsimikiziridwa pamaso panu pomwe, ndi dziko, ndi nthawi, ndi anthu, ndi mwa Mzimu Woyera Umene unalemba Iwo. Izo zatsimikiziridwa, konse kuwiri mwachibadwa, mwauzimu, mwathupi. Chirichonse chimene Iye ananena chakwaniritsidwa ndi kutsimikiziridwa.

<sup>75</sup> Israeli ali m'dziko lake; anawapitikitsira iwo kumeneko, anawalishira iwo kumeneko, monga nkhusa. Mimbulu inamutsatira iye ndipo inawathamangitsira iwo kubwerera ku chitetezero, ku dziko lawo lomwe. Kumbukirani, Israeli anangolonjezedwa kuti adzadalitsidwa pokhapokha iye akakhala kudziko lake. Mulungu samamudalitsa konse Israeli akakhala kunja kwa dziko. Abrahamu anapita kunja kwa dziko, anakaweruzidwako. Aliyense amene achoka m'dzikolo amakaweruzidwa. Mulungu akhoza kokha kumudalitsa Israeli pamene iye akukhala mdziko la kwawo, ndipo ndi uyo ali kumeneko tsopano ngati fuko. Ndipo Mpingo wayitanidwa; iye akungoyembekezera Mkwatulo, wa Mkwatibwi kuti atengedwe.

<sup>76</sup> Zisindikizo zatsegulidwa. Zawululidwa kwa ife. Iye tikuwona zimene iwo anazisiya. Inu amene mukufuna kutsutsana ndi kukangana zokhudza mbewu ya serpenti, ndi ubatizo wa madzi, zina zotero, inu mwachititsidwa khungu ndipo simukudziwa izo. Mulungu wa dziko lino wakuchititsani inu khungu, kwa Iwo, ndipo inu simukudziwa izo. Ndikudabwa ine ndinali ndi nthawi yoteroyo mmawa uno, kumenyana ndi zipsyinjo zimenezo!

<sup>77</sup> Kotero aneneri awo akhoze kuwululidwa mu tsiku lotsiriza lino; sangakhoze kuchita izo, kupyolera mu Malipenga, a... kupyolera mu Phwando la Malipenga.

<sup>78</sup> Iye ananena, kudzera Hoseya, "Ine ndawasema." Tsopano penyani, Israeli Iye akuyankhula naye. "Ine ndamusema," kapena mawu ena, "Ine ndawakhapa, ndawakhapa iwo, kupyolera mwa aneneri." Umo ndi momwe Mulungu amachitira ndi anthu Ake. Iye anawakhapa iwo kuchokera ku mafuko ena onse. Ndi chiyani? Lupanga Lake lakuthwa konsekonse, Mawu Ake. Iye anawakhapa iwo, fuko Lake, kuchokera ku mafuko.

Iye anakhapa fuko Lake kuchoka ku mafuko, pogwiritsa ntchito aneneri, Mawu Ake otsimikiziridwa.

Chomwechonso Iye wamukhapa Mkwatibwi Wake kumuchotsa ku zipembedzo, pogwiritsa ntchito Mawu Ake; olonjezedwa ndi Malaki 4, mu tsiku lotsiriza. Anamukhapa Mkwatibwi Wake, anamudula Iye kuchokera ku mipingo yina yonse! Anamudula Mkwatibwi Wake!

<sup>79</sup> Iye anakhapa, aneneri Ake; kudutsa, ndi aneneri Ake, pogwiritsa ntchito Mawu kumudula Israeli. “Dzipatuleni nokha kwa ena onsewo.”

Tawonani pamene iwo ankafuna kuti azichita monga ena onse a iwo. Iwo anabwera kwa mneneri, Samueli. Iye anati, “Kodi ine ndinayamba ndatengapo ndalama zanu? Kodi ine ndinayamba ndayankhulapo kwa inu mu chirichonse, mu Dzina la Ambuye, koma chimene chinachitika?”

Iwo anati, “Ayi, izo, izo nzoona, koma ife tikufunabe mfumu.”

<sup>80</sup> Umo ndi momwe mipingo yachitira. “Oh, ife timakhulupirira Mawu. Iwo ndi abwino, koma, inu mukudziwa, iwo amati ife tizichita *ichi*.” Sindikusamala zomwe iwo akunena. Mawu ndi owona!

Akudikirira. Iye wawadula iwo, kupyolera mwa aneneri.

<sup>81</sup> Ndi nthawi yanji, m’bale? Ndi nthawi yanji, mtumiki? Kodi inu mukuona nthawi ya tsikuli, ndi chizindikiro chimene inu mukukhalapo? Kodi inu mukukhoza kuzimvetsa izo? Kodi inu mukuziwona izo?

<sup>82</sup> Konsekonse tsopano, kulibeko chitsitsimutso. Aliyense akudandaula, atumiki akulira. Ine ndimawerenga imodzi ya—mapepala opambana amene amabwera kuno ku tchalitchi, pepala labwino kwambiri. Ndipo ine ndikumudziwa mkonzi wake, ndipo ine ndikuwadziwa anthuwo. Ndipo iwo ndi anthu aumlungu, abwino kwambiri, M’bale ndi Mlongo Moore, a *Herald of His Coming*. Imodzi mwa mapepala abwino kwambiri kumundako, *Herald of His Coming*. Koma iwo samasindikiza kalikonse pokhapokha ngati ziri za, “Musale, mupemphere! Musale, mupemphere! Muwombe lipenga! Mupeze. . .” Ndi angati amawerenga zimenezo? Inu mukudziwa. Inu mumaziwona izo nthawi zonse, “Musale, mupempheroe! Musale, mupemphere!” Ndizo zonse zomwe mumazimva. “Musale, mupemphere! Tikhala ndi tsiku labwino kwambiri! Pali chinthu chachikulu chimene chiti chichitike! Nonse a inu, pempherani, pempherani, pempherani! Ife sitinachedwebe!”

<sup>83</sup> Nchifukwa chiyani iwo amachita zimenezo? Nchifukwa chiyani iwo amachita zimenezo? Iwo akufuna kutsitsimuka kwakukulu. Iwo akulira, akukhulupirira kuti padzakhala kutsitsimuka. Iwo ndi anthu abwino. Nchifukwa chiyani ziri

chomwecho? Kodi iwo achita chiyani? Iwo sanakuzindikire kutsitsimuka kwa Mkwatibwi. Mukuona? Pokhala Mkhristu, iwo akumverera kukoka kwa orali, koma iwo sanazindikire chimene chachitidwa. Ndi chimene chikuwapangitsa iwo kumverera chomwecho. Iwo akudziwa kuti chinachake chikuyenera kuchitika, koma, mwaona, iwo akuchiyembekezera icho kutali mtsogolomo, kuti chidzabwera, pamene icho chachitika kale pafupi ndi inu.

<sup>84</sup> Ndicho chinthu chomwecho chimene iwo anachita mmasiku akale. Iwo ankakhulupirira Mesiya wakudza. Iwo ankakhulupirira kuti padzabwera wotsogolera kubwera. Koma izo zinali pa iwo pomwe, ndipo samadziwa zimenezo. Iwo sanazindikire izo. Iwo ankakhulupirira kuti pakanadzabwera wotsogolera amene akanadzamtsogolera Mesiya, ndipo iwo anamdula mutu wake. Ndipo anamupha Mesiya wawo, chifukwa izo zinaloseredwa kuti iwo adzachititsidwa khungu. Hoseya ananena chomwecho.

<sup>85</sup> Ndipo Mzimu womwewo, umene unayankhula kudzera mwa Hoseya, unadzayankhula kudzera mwa Yohane ndipo unati mpingo mmasiku otsiriza ano udzakhala “wamaliseche, ndi wakhungu, ndipo udzamyuka Iye kunja kwa mpingo.” Iwo analephera kuti awawone maulosi amenewo akukwaniritsidwa. Koma, pokhala mmenemo, iwo akuzindikira kuti chinachake chikuyenera kuchitika. Iwo basi sakumvetsa zimenezo. Iwo sakuzindikira zimenezo. Mofanana monga Ayuda a nthawi zakale; Laodikaya wochititsidwa khungu; chuma, zaumulungu, amadana ndi Mpingo, amadana ndi Uthenga. Taonani momwe Ayuda amenewo anali odana ndi Yohane. Taonani momwe iwo anali odana ndi Yesu, pamene Iye anali Mmodzi yemweyo amene iwo ankadzinenera kuti iwo ankamuyembekezera.

[Chowulutsira mawu chikuphokosera—Mkonzi]. Ine ndikukhulupirira kuti taphulitsa fyuzi. Ine ndikuganiza izo zazimitsa zojambulira matepi, nazonso. Sizinatero. Chabwino.

<sup>86</sup> Iwo anali odana ndi Uthenga.

Zomwe zimachitika, ndi mphamvu zochuluka; aliyense wa inu nonse ndi chotenthetsera. Palibe njira yosungira mpingo mwangwiro mu zimenezo, pansu pa nthawi zimenezo. Chifukwa, inu mukuona, aliyense wa inu ndinu nainte-eyiti BTU, mwachizolowezi. Ndipo inu sikuti mumangokhala pamenepo monga choncho; inu mosalekeza mumakhala mukuzimitsa moto. Muli mpweya wokwanira muno tsopano wokhoza kuwumitsa malowa. Koma, ndi chotenthetsera chikuyenda, inu—inu simungachite zimenezo.

<sup>87</sup> Zindikirani, awudani! Koma, tsopano, monga Ayuda akale, anachititsidwa khungu! Iwo ali ku Laodikaya. Iwo ndi “amaliseche, omvetsa chisoni, atsoka, ndipo sakudziwa izo.” Tsiku la chuma, ziphunzitso zazikulu zaumulungu, maphunziro

aakulu, ndipo tsopano iwo asanduka odana ndi Uthenga. Iwo sakufuna kanthu kochita ndi Iwo, chimodzimodzi monga momwe zinaliri mmbuyo mmasiku amene Yesu waku Nazareti anali pa dziko lapansi.

<sup>88</sup> Chifukwa chimene anthu, mu tsiku la Nowa, sanalowe mchombo, chifukwa iwo sanawuzindikire uthenga ngakhale wa mthengayo. Ndicho chifukwa chokhacho chimene iwo anawonongekera, ndi chifukwa chakuti iwo sanazindikire ora limene iwo ankakhalamo. Iwo sanazindikire kuti Mulungu akanadzachita ndi tchimo monga momwe Iye analonjezera kuti Iye akanadzachitira. “Iye adzamuwononga munthu, kumuchotsa pa nkhope ya dziko lapansi.” Iye anali atanenera zimenezo. Iye ankatanthauza izo. Ndipo Iye akutanthauza izo lero chimodzimodzi monga Iye anachitira nthawi imeneyo.

<sup>89</sup> Koma anthu, mmalo momukomera Nowa, iye ankatengedwa ngati munthu wakuthengo. Iwo sanamukhulupirire iye kuti anali mneneri. Inu mukudziwa, Yesu, Mwini Wake Yemwe, anatiuza ife momwe iwo ankanyozera mmasiku a Nowa, ankamunyogodola iye, ankamutcha iye wotengeka ndi zina. Koma iwo sanalizindikire ora lawo. Iwo sanalizindikire tsikulo. Iwo sanachizindikire chizindikiro. Iwo sanawuzindikire uthenga. Iwo sanamuzindikire wa mthengayo, koma anamuchotsa iye pakati pawo ndipo anamuseka iye. Yesu anati, “Monga mmene zinakhalira m’masiku a Nowa!”

<sup>90</sup> Ndi Israeli mdziko lake, ndi chirichonse chitakhala tsopano, ndipo Uthenga ukungosunthira mkati mwangwiro, tikukhala mu tsiku lanji m’bale? Kodi ife tiri kuti?

<sup>91</sup> Iwo sanalidziwe tsikulo. Iwo sanalidziwe. Ndi chifukwa chake iwo analiphonya ilo, ndi chifukwa chakuti iwo sanalizindikire ilo. Iwo anali monga tsikulo, mofanana mochuluka ndi anthu lero, anachititsidwa khungu ndi zitsimikiziro zasayansi, ndi kachitidwe ka maphunziro, ndi maseminare a zaumulungu. Ndipo zinthu zimene zinawachititsa iwo khungu mu tsiku limenelo, izo zachita chinthu chomwecho lero. Izo zawachititsa khungu, kachiwiri.

<sup>92</sup> Ndipo, komanso, kuphweka, kuphweka kwa uthenga ndi mthenga! Nowa sanali wasayansi. Iye sanali munthu wophunzira. Iye anali mlimi wosauka, wodzichepetsa, ali ndi uthenga wophweka. Iwo unali wophweka kwambiri kwa maphunziro awo apamwamba.

Chomwechonso izo ziri lero! Mulungu nthawizonse amazipangitsa izo kukhala zophweka, kuti zikawapeze anthu amene ati adzakhulupirire ndi kumudalira Iye. Ndi wosiyana, Uthenga wosiyana basi, koma Mulungu yemweyo. Tsopano ine ndikufuna kuti inu mukhulupirire Iwo ndi kumvetisa kuti Mulungu wawulankhula Iwo.

<sup>93</sup> Yesu anati iwo anamunyoza mneneri Wake, Nowa. Ndipo monga iwo ananyoza mu tsiku limenelo, chomwechonso iwo adzachita izo kachiwiri pa Kudza Kwake. Iwo akanadzachita chinthu chomwe chomwecho.

Ndi chifukwa chake Farao anamira mnyanja. Iye sanalizindikire konse tsiku lake. Iye sanazindikire chimene chinkachitika. Iye anali atatengeka kwambiri ndi zokwaniritsa za m’badwo wake wasayansi, kuti amange mizinda ndi ntchito za ukapolo. Iye anali kwambiri—anali wotanganidwa kwambiri, kuti awuzindikire mwayi umene anali nawo, ndipo iye anampitikijsira mneneri-mthenga wa Mulungu ku chipululu. Iye sanazindikire zimenezo. Icho ndi chifukwa chake zinthu zinayenda momwe izo zinachitira. Iye sanazindikire izo nkomwe. Ngati iye akanangozindikira Mawu olonjzedwa a Mulungu, kwa anthu amenewo!

<sup>94</sup> Ndipo ngati mipingo lero ikanangozindikira, ngati mipingo ikanangozindikira Mawu a Mulungu omwe apanga lonjezo ili la ora lino, kwa anthu, iwo sibwenzi atawonongeka.

Ngati America akanangozindikira malamulo omwe anawapanga, iye sakanalolera kuti ahotse Mabaibulo kuchokera mmasukulu, kulichotsa Dzina la Mulungu pa ndalama, ndi lonjezo lokhulupirika pansu pa Mulungu. Koma iye sakuzindikira izo. Chifukwa chiyani? Iye ndi wakhungu, wamaliseche. Iye akulephera kuzindikira magazi a anyamata ofunika amenewo amene anafera m’minda chifukwa cha mwayi uwu. Iwo anayiwaliika; iwo ndi fumbi.

<sup>95</sup> Koma alipo Mmodzi Amene amakumbukira kukhetsedwa kwa magazi a aneneri, mtengo umene unatengera kuti abweretse Uthenga uwu kwa ife lero. Momwe masauzande anadyedwa ndi mikango, ndi kuponyedwera mmphanga, anachekedwa pakati, kuwotchedwa, kupachikidwa! Mulungu amazindikira zimenezo.

Mpingo unawaiwala aneneri awo. Iwo “sakuwafunanso iwo,” iwo amadzinenera chomwecho. Koma Mulungu akudziwa kuti Iye ayenera kukhala nawo iwo; Iye amadula anthu Ake ndi Mawu Ake. Koma Iwo ndi achikale kwambiri kwa iwo mu tsiku lino. Iwo samawazindikira Iwo. Ndi chifukwa chake iwo ali mu chikhalidwe chimene iwo alimocho. Ndi chifukwa chake iwo ali “amaliseche, omvetsa chisoni, akhungu, atsoka, ndipo sakuzidziwa izo,” chifukwa iwo sakulizindikira ora limene ife tikukhalamo. Iwo sakulizindikira ilo.

<sup>96</sup> Mose, iye analizindikira tsiku lake ndi mayitanidwe ake, pamene iye anawona lonjezo la Mawu a Mulungu la tsiku limenelo likutsimikiziridwa. Iye anadziwa pamenepo, ndipo anazindikira chimene iye anali ndi chimene iye anali woti adzachite, mwa Mawu olonjzedwa. Kotero iye sanawope chimene aliyense ankanena. Iye sanachite manyazi ndi uthenga wake, ngakhale wansembe aliyense ndi farao aliyense,

chirichonse, ulamuliro uliwonse, zinkatsutsana naye iye. Koma iye anazindikira pamene anadzawona Kuwala kuja, Lawi la Moto lija litapachikika mchitsamba chija, ndipo chinayankhula ndi iye Mawu amene analonjezedwera tsiku limenelo, ndipo anati, “Ine ndakuyitana iwe kuti upite ukachite zimenezo.” Iye sanawope—zowopsyeza zazikulu za mfumu. Iye anapita kumusi kuti akawabweretse anthu amenewo ku kutuluka, monga momwe Mawu a Mulungu analonjezera.

<sup>97</sup> Atawona lonjezo likutsimikizidwa, iye anawakonzekeretsa anthu ku kutuluka kwawo. Liti? Pamene iye anawona lonjezo la Mulungu likutsimikizidwa. Kumbukirani, iye ankathamanga ndi zaumulungu zake; ankathamanga ndi maphunziro ake. Koma pamene iye anawawona Mawu a Mulungu akuwonetseredwa, iye anawawona Iwo akutsimikizidwa, “INE NDINE AMENE NDIRI INE,” ndiye iye sanasamale zomwe aliyense ankanena. Iye sanawope zimene Farao akanadzachita naye iye. Iye sanawope zimene ena a iwo akanadzachita. Iye anangowopa Mulungu, kuti iye akhoza kusamumvetsa Mulungu, kapena njira ina imene iye akanakhoza kusamumvetsa Mulungu. Iye sankawawopa anthu ndi zomwe akanadzanena kapena zomwe akanadzachita. Iye ankomuwopa Mulungu, iye atazindikira kuti awo anali Mawu a Mulungu.

<sup>98</sup> Iye samamvetsetsa momwe munthu ngati iyeyo angatumizidwe kumusi kumeneko. Koma pamene iye anazindikira, mwa Mawu otsimikizidwa, chimene icho chinali, pamenepo iye sanawope malamulo a mfumu. Ngati inu mutangozindikira, ngati ife lero titangozindikira! Mose anazindikira izo pamene iye anawawona Mawu akutsimikizidwa, anawona kutsimikizidwa kukutsimikizidwa, Iye anali atakonzekera kutuluka kwa anthuwo.

Yobu sanazindikire konse kuti uyo anali Mulungu. Bola ngati mdierekezi anga—angakupangitseni inu kukhulupirira nthawi ina kuti mayesero aang’ono omwe inu mukudutsamo ndi—ndi Mulungu. . . akukulangani inu! Anali Mulungu akuyetsa kuti amuwonetse iye chinachake. Yobu sanazindikire icho mpaka iye atawona masomphenya. Monga Mose; pamene Mose anawona masomphenya, Lawi la Moto mu chitsamba, izo zinatsimikizidwa. Ndipo pamene. . .

Yobu, mu funso lake, “Ngati munthu afa, angadzakhalenso ndi moyo? Ndimawona mtengo utafa, ndipo umadzakhalenso moyo. Ine ndimawona duwa litafa, ndipo limakhalenso moyo.” Limenelo linali funso lake. “Koma munthu amagona pansi, iye amataya mzimu, amatayika. Ana ake aamuna amabwera kudzalira, koma iye samazidziwa zimenezo. Oh, kuti Inu mudzandibise ine mmanda mpaka mkwiyo Wanu utapita!” Iye samamvetsa chifukwa chiyani duwa limafa ndi kudzakhalenso moyo, momwe tsamba limathothokera pantengo, pansi,

ndi kugona pansi, ndi kudzabwereranso mu kuphukira. Iye anati, “Munthu amagona pansi, ndipo iye amapita kuti? Ine ndimakhulupirira Mulungu; koma chimachitika ndi chiyani kwa munthu?”

<sup>99</sup> Komano tsiku lina mphezi inayamba kung’anima, mabingu anayamba kubangula, Mzimu unadza pa mneneri. Ndipo iye anawona kudza kwa Munthu Amene akanakhoza kuyika dzanja Lake pa munthu wochimwa, ndi Mulungu woyera, ndi kulumikiza njirayo. Kenako iye anafuula, “Ndikudziwa Muomboli wanga ali moyo! Ngakhale mphutsi zitawononga thupi ili, komabe mu thupi langa ine ndidzamuwona Mulungu!” Iye anazindikira chimene chiukitsiro chinali.

<sup>100</sup> Balamu sanamuzindikire konse Mngelo kufikira bulu atayankhula mmalirime. Balamu sakanatha kuzindikira kuti Mngelo wayima panjira yake. Mlaliki wochititsidwa khungu sakanatha kuzindikira kuti anali Mulungu atayima panjirapo, akuyesera kuti amuletse iye kugulitsa mphatso yake ndi ndalama. Ndipo pamene buluyo atayankhula ndi liwu la munthu, kenako Balamu anazindikira kuti anali Mngelo amene anayima pa njira yake, akuyesetsa kuti amuletse iye kuti asachite chimene iye ankachita.

<sup>101</sup> Oh, inu zipembedzo zochititsidwa khungu! Ngati Mulungu angagwiritse ntchito bulu, amene ndi wosayankhula, kuti ayankhule mu chinenero chimene iye sakuchidziwa, kuti awulule kwa mtumiki kuti iye wachoka panjira, kodi Iye sangamgwiritse ntchito munthu kuti achite chinthu chomwecho? Anthu ochititsidwa khungu!

<sup>102</sup> Ngati Ahabu akanangozindikira tsiku lake, iye sibwenzi atamutsutsa konse mneneri, Mikaya, ndi Mawu a Mulungu a lonjezo kwa iye.

<sup>103</sup> Pamene Ahabu anayima pamenepo tsiku limenelo, iye ndi—ndi Yehosafati. Ndipo pamene iwo anali ndi aneneri foro handirede kunja uko akunenera, akuti, “Kwerani mmwamba! Zonse ziri bwino. Ahabu, iwe ukukhala mu tchimo. Iwe watipanga ife kukhala chipembedzo chachikulu! Ndife anthu abwino. Ndife utumiki waukulu. Ndi ife apa, ndife ansembe foro handirede ophunzitsidwa, kapena aneneri. Ndife foro handirede, ophunzitsidwa mu Mawu ndi zaumulungu. Ife tikudziwa zonse za Iwo.”

<sup>104</sup> Kotero, tsopano, izo zinatsimikizira kuti iwo sankadziwa zonse za Iwo. Munthu amene iwo ankamutcha munthu wopenga, mu kam’badwo pambuyo pawo, Eliya, mneneri woona wa Mulungu, anali atanenera, “PAKUTI ATERO AMBUYE, ‘Agalu adzanyambita magazi ako, Ahabu!’” Mukuona?

<sup>105</sup> Koma ansembe amenewo, aneneri opangidwa ndi anthu, ankaganiza kuti iwo anali atawakonza Iwo onse molondola basi. Iwo anati, “Atate Abrahamu...kapena, Atate Ahabu, pitani



kumeneko! Ambuye ali ndi inu. Inu muli ndi Lembu, chifukwa Mulungu anapereka dziko ili kwa Israeli. Ilo ndi la Israeli. Pitani uko! Ambuye ali ndi inu.” Oh, mai!

<sup>106</sup> Koma, inu mukudziwa, Yehosafati, mmodzi yemwe anali asanazipiringize mu tchimo monga Ahabu anachitira, iye ankawona zinthu mosiyana pang’ono. Iye anati, “Kodi palibenso wina?”

<sup>107</sup> Iye anati, “Ife tiri ndi mmodzi kuno, koma ine ndimamuda iye.” Mukuona? Kodi Mulungu anali akuchita chiyani? Kuwadula anthu Ake, ndi mneneri, kachiwiri. “Ine ndimamuda iye. Iye samachita kalikonse koma kumangondidzudzula nthawi zonse. Ndipo iwe ukudziwa kuti ndine munthu wamkulu. Ine sindikanakhala ndi seminare iyi kumusi kuno ngati ndikanati ndisakhale wokhulupirira wamkulu. Ndiri ndi amuna ophunzitsidwa bwino. Ine ndawakhazika iwo uko ndi mabukhu ndi Mabaibulo, ndi china chirichonse, kuti aziphunzitsa izi. Ndipo ndikudziwa kuti iwo ndi anthu opambana.”

Koma ngati Ahabu akanangozindikira yemwe munthu ameneyo anali, munthu wamng’ono wooneka-wosauka uyu, mwana wa Imla, atayima pamenepo, akumuuya iye, “PAKUTI ATERO AMBUYE,” iye sibwenzi atapanga konse kulakwitsa kowopsya komwe iye anachitako. Koma iye anamutsutsa Mikaya. Iye sanatero konse . . .

Oh, anthu, zindikirani m’badwo umene inu mukukhalamo! Onani zomwe zachitika. Onani zomwe zalonjezedwa. Zindikirani tsiku limene mukukhalamo.

<sup>108</sup> Ngati chipembedzo cha mpingo lero chikanangozindikira chifukwa chimene iwo akutsutsidwa, ndipo mamembala awo akuwathawa iwo, monga Israeli akutuluka mu Igupto! Ngati zipembedzo zikanangosiya kuwatsutsa matepi amenewo, ndipo zikanamawamvetsera iwo! Ndipo iwe, mlaliki, ukumvetsera tepi iyi, iwe uyimvetsera! Ngati inu mukanangozindikira ora limene inu mukukhalamo, ngati inu mukanangozindikira chizindikiro cha nthawiyi, inu mukanawona chifukwa chimene anthu akuthawa kuchoka ku zipembedzo zimenezo. Mzimu wa Ambuye, ukuyitana! “Palibe munthu angabwere kwa Ine,” Yesu anati, “pokhapokha Atate Anga atamukoka iye. Ndipo onse amene Atate ali nawo, mu nthawi zakale, andipatsa Ine, adzadza.”

<sup>109</sup> Monga mkazi wamng’ono pachitsime, ndi wansembe, momwe iwo anali osiyana! Cholembedwa chiri pakhoma la lero, kachiwiri. Iwo akuchiwona icho, koma iwo sakuchizindikira icho.

<sup>110</sup> Ngati Ayuda akanangozindikira chizindikiro cholonjezedwa cha Mesiya wawo, mogwirizana ndi mneneri wawo wotsiriza! Malaki 3 anati, “Taonani, ndidzakutumizirani wa mthenga

Wanga patsogolo pa nkhope Yanga, ndipo adzakonza njira.” Ndipo iwo ankadzinenenera kuti iwo ankamuyembekezera Iye.

<sup>111</sup> Ndi a—ndi kufanana kwenikweni bwanji ndi—ndi lero! Iwo amanena kuti akuyembekezera chinachake kuti chichitike. Mpingo yonse ikupemphera ndi kusala, ndi kumati, “Tsopano tiyeni tipemphere. Tiyeni tisonkhane pamodzi. Iye tiyenera kukhala ndi chinthu chachikulu choti chichitika. Tikudziwa kuti pali chinachake chachikulu choti chichitike. Mpingo ukuyenera kukonzekera.” Icho ndi chimene iwo akuchipempherera.

<sup>112</sup> Ndi chimene iwo ankachipempherera kumeneko. Ndipo pamenepo panadza Yohane M’batizi. Chifukwa, iye anakana maseminare awo, chifukwa iye ankachita zotsutsana ndi zimene makolo awo anaphunzitsa. Iye anatuluka m’chipululu wopanda maphunziro. Iye anatuluka wopanda kolala yake itatembenezidwa, monga zinganenedwere lero. Iye anatuluka wopanda mulu waukulu wa zaumulungu. Koma iye anabwera, akudziwa mwa lonjezo la Mulungu kuti iye anali woti alengeze Mesiya.

Iye anati, “Iye akuyima pakati panu tsopano.” Ndipo iwo ankaganiza kuti iye anali wopenga, chifukwa iye sanabwera kuchokera ku masukulu awo. Cholembedwacho chinali pakhoma, ndipo iwo samadziwa zimenezo. Iwo ankadzinenenera kuti ankayembekezera Munthu woteroyo kuti abwere; ndipo Iye anali pakati pawo pomwe. Ndipo iwo sanamuzindikire Iye, ngakhale iwo anati iwo ankamuyembekezera Iye.

<sup>113</sup> Basi chimodzimodzi, monga Ayuda, kuti iwo ali, monga Amitundu ndi awo, chifukwa izo zinaloseredwa chinthu chomwecho, chinthu chomwecho. Ankadzinenenera kuti ankamuyembekezera Iye. Koma zipembedzo tsopano mwa Amitundu, m’badwo wa Laodikaya ndi wakhungu basi monga iwo anali, chifukwa (chifukwa chiyani?) zinaloseredwa kuti iwo akanadzakhala. Izo zikuyenera kudzachitika.

<sup>114</sup> Ngati Israeli akanangozindikira chizindikiro chawo, iwo akanadziwa kuti nthawi ya kuwonekera kwa Mesiya inali pafupi. Ngati iwo akanazindikira!

Inu mukudziwa, o—ophunzira ananena zimenezo kwa Yesu. “Nchifukwa chiyani alembi amanena kuti, ‘Eliya akuyenera kubwera poyamba?’”

<sup>115</sup> Ndipo Yesu anati, “Eliya anabwera kale, ndipo iwo sanamudziwe iye. Iye ali kale kuno, ndipo iwo amupha kale iye. Iwo anachita chimodzimodzi basi chimene Lemba linati iwo akanadzachita.”

<sup>116</sup> Ngati iwo akanangozindikira, kuti “wotengeka” ameneyo amene anatsutsa zinthu zowirikiza zonse zimene iwo amachita, amene anatsutsa chirichonse chimene iwo ankachita...Iye anati, “Onyenga inu! Musayambe ku...Njoka mu udzu, inu kam’badwo ka njoka, wakuchenjezani ndi ndani kuti muthawe

mkwiyo umene ulinkudza? Musayambe kuganiza mwa inueni, 'Ife tiri naye Abrahamu atate wathu. Ife tiri ndi *ichi, icho*, kapena *chinacho*.' Pakuti ndikukuuzani inu, Mulungu ndi wothekera mwa miyala iyi kuwukitsa ana kwa Abrahamu."

<sup>117</sup> Musayambe kuganiza kuti muli ndi World Council m'manja mwanu, ndipo inu muli ndi mamembala ovala bwino a zimenezo. Mulungu ndi wokhoza mwa makoswe a mngalande kunja kuno kudzutsa ana kuti akwaniritse Mawu Ake; aziwerewere, oyenda m'misewu, zidakhwa, otchova njuga. Iye ndi wokhoza kuchita izo. Iye akadali Mulungu.

<sup>118</sup> Zipembedzo zochititsidwa khungu, monga Israeli wochititsidwa khungu, ziwiri zonse zinaloseredwa kuti zidzakhala mwanjira imeneyo. Ine ndikukuwonetsani inu zofanana zake, mpaka ine ndifike pa malo awa amene ine ndikuwafuna tsopano. Ochititsidwa khungu, monga—zipembedzo za Amitundu za M'badwo wa Laodikaya, zachititsidwa khungu lero monga zinaliri nthawi imeneyo.

<sup>119</sup> M'badwo wa Laodikaya ukuyenera kulandira Uthenga! Malaki 4 anati iwo adzatero.

Koma kodi iwo akufunafuna chiyani? "Chipembedzo chathu chidzatulutsa Iwo. Ngati Iwo subwera kudzera mwa ife, Abaptisti, Apresbateria, a—Assemblies, a Umodzi, pali a... ngati ife sitikuwupereka Iwo, Iwo si woona."

Chinthu chomwecho chimene iwo anachita mu tsiku limenelo! Ndipo icho chinadzabwera ndipo chinapita, ndipo iwo sanadzawe zimenezo. Iwo sanachizindikire icho, ngakhale icho chinakwaniritsa Mawu aliwonse. Yesu anati, "Iwo achita monga momwe zinalembedwera kuti iwo akanadzachita. Momwemonso iwo adzachita kwa Mwana wa munthu," Iye akanadzakanidwa.

<sup>120</sup> Tsopano zindikirani, chimodzimodzi tsopano mmasiku a Amitundu, molingana ndi Malemba olonjezedwa a Malaki 4.

Chimene, Yesu anati, "Malemba onse ndi odzodzedwa, ndipo palibe gawo limodzi la Iwo lomwe lingalephere kukwaniritsidwa." Palibe njira yolepheretsa Malemba kuti asakwaniritsidwe. Onse akuyenera kukwaniritsidwa. Ndipo Yesu anati izo zikanadzachitika. Ndipo apa ife tikuziwona izo zinachitika. Ife tikuziwona izo.

<sup>121</sup> "Kubwezeretsa" chiyani, mmasiku otsiriza ano? Inu abale azipembedzo, mveterani! Kubwezeretsanso phwando lachipentekoste, lapachiyambi. Monga Izo zinali pachiyambi, chomwechonso Izo zidzabwezeretsedwa phwando la Lipenga la Israeli lisanawombe. Zikuyenera kubwezeretsedwa! Pakuyenera kukhala chinachake choti chidzachite izo. Malaki 4 anati izo zikanadzabwezeretsanso Chikhulupiro cha atate, kwa ana, chimene chikanati chidzachitike.

<sup>122</sup> Ngati Israeli akanamuzindikira Mesiya wawo, chizindikiro cholonjezedwa, iwo sibwenzi ali pamene iwo ali lero. Ngati iwo akanatero. . . Koma nchifukwa chiyani iwo sanachite zimenezo? Izo ndizomvetsa chisoni. Nchifukwa chiyani iwo sanachite izo? Chifukwa Mulungu anati iwo sakanadzachita izo. Ndi angati akukhulupirira zimenezo, nenani, “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Mulungu anati iwo sakanadzachita izo.

Ndipo ndi Mulungu yemweyo wanena, mu M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya, izi zikanadzachitika, ndipo ndi izi apa pamaso pawo. Kodi iwo angachite bwanji china chirichonse koma kuchichita icho?

<sup>123</sup> Ngati iwo akanangozindikira chizindikiro cholonjezedwa cha Mesiya, chizindikiro cha Mwana wa munthu! Iye anabwera mu dzina la Mwana wa munthu. Tsopano, Iye anali mu dzina, kudutsa mu M’badwo wa Pentekoste, mu Mzimu Woyera, Mwana wa Mulungu. Tsopano, chinthu chotsatira ndi Zakachikwi, Mwana wa Davide. Atatu “Ana,” Mulungu yemweyo. Yemweyo, “Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” Mulungu yemweyo. Mwana wa Davide, Mwana wa Mulungu. . . Mwana wa Davide, Mwana wa munthu, Mwana wa Mulungu, ndi Mulungu yemweyo nthawi zonse, basi mu ntchito za maudindo atatu zosiyanasiyana.

<sup>124</sup> Momwemonso ndi “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera” osati Amulungu atatu, koma Mulungu yemweyo mu nyengo zitatu, ntchito za maudindo atatu, monga Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.

Koma, monga lero, achititsidwa khungu ndi miyambo monga iwo anachitira kumeneko, achititsidwa khungu ndi miyambo, iwo sakuziwona zimenezo. Chifukwa chiyani iwo sakuziwona izo? Iwo sadzaziwona konse izo. Kumbukirani, ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE.

Mukuti, “Nchifukwa chiyani inu mukunena zimenezo ndiye?”

Chimodzimodzi basi monga Yohane anachitira, chimodzimodzi monga ena onsewo anachitira. Pali chimodzi chobaya apa ndi apo, chimene chiyenera kutulutsidwa. Oh, nkhosa za Mulungu, imvani Liwu la Mulungu! “Nkhosa Zanga zimamva Liwu Langa.”

<sup>125</sup> Mkazi pa chitsime anazindikira tsiku lake, mwa chizindikiro cha Mesiya. Iye anali mchikhalidwe choipa. Iye sanafune kuti azipusitsidwa ndi mipingo yakale iyo, momwe iwo ankachitira. Iwo ankangokhala mulimonse, ndipo, zinthu zimene iwo ankachita, iye samakhulupirira zinthu zimenezo. Koma iye ankadziwa kuti kudzabwera Mmodzi tsiku lina. Munthu wamng’ono wosawuka kumtunda uko, panjira yopita ku chitsime; iye anapeza Chinthu chomwe ankachifuna, pamene Iye anayamba kuwulula kwa iye chinsinsi cha mtima wake, anamuza iye tchimo limene iye ankakhalamo.

Iye anati, “Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndi Mneneri.” Tsopano, iwo anali asanakhale ndi mmodzi kwa zaka foro handiredede. Anati, “Ine ndazindikira kuti Inu ndi Mneneri. Ndipo ine ndikudziwa kuti pamene Mesiya adzabwera Iye adzachita zinthu izi.”

Iye anati, “Ine ndi Iyeyo.”

<sup>126</sup> Iye anazindikira. Apo panalibenso funso lina, “Mungatsimikizire motani zimenezo Inu?” Izo zinali zitatsimikiziridwa kale. “Pamene Mesiya adzabwera, ichi ndi chimene Iye ati adzachite.”

Chabwino, ngati iye angazindikire izo mwa Malemba, kodi ife sitingazindikire Kuwala kwa kumadzulo ndi chizindikiro cha lero?

“Ife tikudziwa pamene Mesiya adzabwera Iye adzatiwonetsa ife zinthu zonsezi. Iye adzatiuza izi.”

Iye anati, “Ine ndine Iye amene ndikuyankhula ndi iwe.”

<sup>127</sup> Panalibenso funso. Iye anapita, ndipo iye anakawuza anthu, “Bwerani, mudzamuwone! Iye ali kuno.” Panalibenso funso kwa iye. Izo zinali zitakhazikika, chifukwa iye anazindikira tsiku limene iye ankakhalamo. Iye analizindikira ilo.

<sup>128</sup> Chomwechonso anachita Nataniele, Mhebri wamkulu, pamene iye anawona chizindikiro chija cha Mesiya chimene chinalonjezedwa kumeneko; zinalibe kanthu ansembe angati, angati china chirichonsecho.

Kodi izo zinachita chiyani? Izo zinawasokoneza ansembe, kuwawona anthu amenewo akuchoka m’mipingo ndi kumapita. Iye anati, “Ngati aliyense wa inu apita ku msonkhano Wake, inu mudzachotsedwa. Ife tidzakuchotsani inu kumene mu chipembedzo.”

<sup>129</sup> Ziri chomwechonso lero. “Ife tidzakutulutsani inu mu bungwe lathu ngati mudzapita ku msonkhano wake.”

<sup>130</sup> Mukukumbukira munthu wakhungu uja? Atate ndi amayi samatha nkomwe kuyankha; iwo ankachita mantha. Chifukwa, iwo anati, “Aliyense amene adzapite kukamuwona Yesu, kapena—kapena kudzakakhala pa misonkhano Yake, iwo adzachotsedwa.” Koma, munthu wakhungu uyo anakhoza kudziyankhulira yekha, iye amene poyamba anali wakhungu anakhoza kupenya.

<sup>131</sup> Ine, amene poyamba ndinali wakhungu, tsopano ndikuwona. Ine, amene sindinkadziwa zinthu izi, Izo zadziwika kwa ine mwa Mzimu Woyera. Masukani, zipembedzo, chifukwa izo zikubwera, mulimonse! “Ngati Ine ndidzakwezedwa kuchoka pa dziko lapansi, Ine ndidzakokera anthu onse kwa Ine.”

<sup>132</sup> Nataniele anazindikira izo. Iye ankadziwa izo.

<sup>133</sup> Basi monga maumboni a Mose a Mwamalemba, Mawu otsimikiziridwa. Mose anadziwa kuti limenelo linali lonjezo la tsikulo, chifukwa ilo linali Mwamalemba, ziribe kanthu zachirendo chotani. Iye anati, “Ine ndimuuze ndani... Ine ndiwauza iwo kuti ine ndinawona Kuwala kumbuyo kuno mchipululu. Ine ndingawawuze bwanji iwo tsopano kuti kunali Kuwala kumbuyo kuno, ndipo Kuwala uku kunandiuza ine kuti ndipite kumusi kumeneko?”

Iye anati, “Ndithudi, Mose, ine ndidzakhala ndi iwe.” Osati kokha...

<sup>134</sup> Iye sanadziwonetsere Yekha ku Igupto; kokha mwa zozizwitsa ndi zizindikiro. Koma pamene Iye anawasonkhanitsa iwo onse pamodzi, Iye anawonekeranso kwa iwo, ndipo anatsimikizira utumiki wa Mose pamaso pa Osankhidwa ndi oyitanidwa-atuluke. Pamene mneneri ameneyo anali atawakhapa iwo kuwamasula ku fuko limenelo ndi kuwabweretsa iwo pamalo, ndiye Lawi la Moto linadzawonekera kachiwiri, ndipo pamwamba pa Phiri la Sinai.

<sup>135</sup> Zikufanana ndi lero. Hmm. Amen! Matamando akhale kwa Mulungu! Izo ndi zoposa moyo kwa ine. Usinkhu wanga ukuyamba kukwawiramo, ndipo ine ndikuwona ora la zonyansa ndi zachiwerewere zikusesa mayiko ndi zinthu, kenako ndikuyang’ana mmbuyo ndi kuwona zomwe zachitika. Mtima wanga umadumphwa ndi chisangalalo, podziwa kuti pakapita kanthawi kachisi wa padziko lapansi wokhalamo uyu adzaphwasuka, koma ine ndiri naye wina akundiyebekezera kutaliko. Ine ndikuyesetsa kuwakokera anthu, kuwakhapa iwo ku zinthu izi ndi zinthu, kuti ndiwakokere iwo kunjja; kuti ndiwawonetse iwo, mwa Malemba, kuti Mulungu wayima pamenepo; ndi chitsimikiziro cha Lawi la Moto, lomwe anthu mahandirede ndi masauzande analiwona, ndipo ngakhale analijambula Ilo, kale, ndi kamera, nthawi ndi nthawi, kuti atsimikizire izo.

<sup>136</sup> Otsanzira amawuka. Ndithudi, izo zikuyenera kuchitidwa. Otsanzira anawuka mu tsiku la Mose ndipo anachita chinthu chomwecho. Mulungu anati, “Dzipatule wekha, Mose. Usakhale pafupi ndi iwo. Ine ndiwameza iwo.” Ndipo dziko linawapeza iwo. Ndi momwemonso izo ziri lero; kubwerera mmbuyo mdziko, ndondomeko zandalama ndi china chirichonse. Mukuona?

<sup>137</sup> Chizindikiro cha Mwamalemba cha Mose! Iye anali—iye anali mneneri wamkulu wa Mulungu uja yemwe anapita kumeneko kuti akawawombole iwo, ndipo iwo anazindikira izo. Iwo anachizindikira chizindikirocho. Iye anali lonjezo lenileni la Mwamalemba, lotsimikiziridwa.

<sup>138</sup> Yesu anali lonjezo lija la Lemba, lotsimikiziridwa kwa mkaziyo. Kapena, Iye anali Kutanthauzira. Yesu

anali Kutanthauzira kwa Lemba. Moyo Wake Womwe unkatanthauzira Lemba.

<sup>139</sup> Kodi inu simukuwuwona Uthenga wa orali? Kodi mukuzindikira kumene ife tiri? Uthenga pawokha, wochokera mu Lemba, umatanthauzira kwa inu ora limene ife tikukhalamo. Ndi kutanthauzira.

<sup>140</sup> Yesu anati kwa Israeli, “Ngati mukadangolidziwa tsiku lanu.” Nthawi ina, atakhala pa Phiri la Azitona, Iye anayang’ana uko, anati, “Yerusalemu, O Yerusalemu!” Iye analira. Iye anayang’ana pansi. Iye anawona.

Osati mu kufanizira kulikonse, mwinamwake, mwanjira. Usiku wina, mmawa wina, pafupifupi teni koloko, pamene ine ndinawona mpingo wachiwerewere uja. Pansi mu mtima mwako, iwe umamva Mzimu Woyera ukugwetsa misozi.

“Yerusalemu, O Yerusalemu, ine ndikanakufungatira iwe kangati. Koma kodi inu munachita chiyani? Inu munapha aneneri amene ndinawatumiza kwa inu. Inu munawapha iwo.”

Ndipo Mauthenga atumizidwa kwa mpingo, lero, aphedwa ndi mbalume zawo zachipembedzo. Lemba laphedwa ndi mbalume zawo. Yesu anati, “Ngati inu mukanangodziwa tsiku lanu! Koma, izo ziri patali kwambiri tsopano, nthawi yatha tsopano.” Momwemonso izo ziri ndi mpingo!

<sup>141</sup> Ine ndikukhulupirira, ndi mtima wanga wonse, iwo wadutsa chiwombolo. Ziribe kanthu zomwe mukufuna kuganiza za izo, ndi maganizo anu. *Awa* ndi anga. Mukuona? Inu simukusowa kukhala ndi lingaliro langa. Koma ine ndikukhulupirira iye wadutsa chiwombolo, ndipo wakhala, kwa zaka faivi kapena sikisi zapitazi. Ine ndikukumbukira. Inu mukukumbukira Chicago. Onani chimene chinachitika kuyambira pamenepo, ndipo muone izo zikupitirira kuchitika. Mukuona? Kumbukirani, dzina langa liri pa izo. Ilo lakakamira pamenepo. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Muone ngati iye sanagwe, pitirizani.

<sup>142</sup> Tayang’anani pa 1933, momwe izo zikunenera kuti akazi akanadzachita mu masiku otsiriza ano. Momwe izo zinanenera kuti anthu. . . Momwe Mussolini, momwe iye akanadzafikira ku mapeto ake. Momwe Hitler akanadzafikira ku mapeto osamvetseka. Momwe kuti ma ism atatu akanadzabwera mu chikominisi. Momwe makinawo adzabwerere, akuwoneka ngati dzira. Ndi momwe akazi azidzavala zovala ndi kumawoneka ngati amuna, ngakhale monga zovala zawo zamkati; ndipo potsiriza adzafika poyika masamba a mkuyu, mokhala ngati, pa iwo. Momwe mchitidwe woyipa, momwe iwo akanati adzachitire mu tsiku lino. Taonani zomwe iwo achita. Ndipo izo ziri pamaso panu pomwe, ndiye.

<sup>143</sup> Ngati akazi Achikhristu akanatha kokha. . . otchedwa akazi Achikhristu akanangozindikira, akanazindikira kuti mzimu

woyipa umene uli pa iwo ndi wa mdierekezi, kuti uwapangitse iwo kumeta tsitsi lawo. Mdierekezi ndi chinthu chokhacho chimene chingachite zimenezo. Ndizo zotsutsana ndi Mawu a Mulungu kwa inu, monga momwe zinaliri m'munda wa Edeni. Kodi iwo anachita chiyani? Ngati iwo akanangozindikira! Iwo amayesera kunena, "Oh, mlaliki wamng'ono wakale woyera wodzigudubuza uja, akuti!" Si ine. Ine sindikukuuzani inu choti muchite. Ine ndikungobwereza Mawu. Ngati iwo akanangozindikira kuti ameneyo ndi mdierekezi.

<sup>144</sup> Iwo amadzitcha okha Akhristu. Yesu anati, "Inu mumanditcha Ine bwanji, 'Ambuye,' ndipo osachita zinthu zimene Ine ndimanena kuti muchite?" Iwo sangakhale Akhristu. Sindine woweruza wawo, koma ine ndikungonena zomwe Mawu ananena. "Inu mumanditcha Ine bwanji, 'Ambuye,' ndiyeno osachita zinthu zimene Ine ndanena kuti muchite?" Ndipo Mawu onse apa ndi vumbulutso la Yesu Khristu. "Inu mumanditcha bwanji Ine, 'Ambuye?'"

<sup>145</sup> Ngati iwo akanangozindikira kuti ndi mdierekezi, mzimu woyipa. Akazi ena aang'ono abwino kunjaku uko. . .

<sup>146</sup> Ine ndikuganiza kuno ndi malo onyansa kwambiri omwe ine ndinayamba ndawawonapo mmoyo wanga, Jeffersonville, Indiana, a akazi osavala. Ndakhalapo ku Hollywood. Ndakhalapo kulikonse. Ndakhala padziko lonse lapansi, ndipo ndawona mitundu yonse ya zonyansa. Ndinaziwona izo ku Paris. Ndinaziwona izo ku England, yemwe ali wamkulu wa onsewo.

<sup>147</sup> Ndikuganiza kuti England idzamizidwa tsiku lina pansu pa nyanja. Iyo ikuyenera izo; nyansi, zodetsedwa, zonyozeka! Ndicho chithaphwi cha makhalidwe oyipa cha mdziko, anthu opanda malemba kwambiri owakananso, amene ndinayamba ndawawonapo mmoyo wanga. Iye wakhala icho chifukwa iye wakana Choonadi.

<sup>148</sup> Billy Graham anati iye anachita kumuchotsa mkazi wake ku malo opumirirako; zinthu zogonana zikuchitika pakati pa amuna ndi akazi, anyamata ndi atsikana, kunjaku komwe ku malo opumirirako, mosabisa. Iye wakhala chithaphwi; chomwechonso France, chomwechonso dziko lonse lapansi. Ndipo chomwechonso United States, akukhala mtsogoleri wa iwo onsewo!

<sup>149</sup> Tayang'anani lero. Akuwapangitsa iwo kumeta tsitsi lawo, kuvala akabudula, zazifupi, kusuta, ndi kumadzitcha okha okhulupirira. Kodi inu simukuzindikira, mlongo, kapena mkazi. . .Ndikutanthauza, mundikhululukire, osati mlongo wanga; kuchita chinthu choterocho. Kodi inu simukuzindikira kuti ndi mdierekezi? Koma chimene. . .

Monga Ayuda akale, inu simudzakhulupirira Mawu otsimikiziridwa pamene Iwo atsimikiziridwa kwa inu. Inu



mumakangamira ku miyambo yanu yachipembedzo imene imati izo nzabwino. Inu mumayankhula mmalirime, inu mumalumpha lumpha, inu mumayimba mu mzimu, ndi kumadula tsitsi lanu. Kodi inu mungalingalire Mkristu kumachita zimenezo?

Ine ndawonapo adierekezi, ine ndawawonapo asing'anga, ine ndawawonapo iwo akuyankhula mmalirime ndi kutanthauzira, ndi kumalumpha lumpha ndi kumavina mu mzimu; kumwa magazi kuchokera mu chigaza cha munthu, ndi kutemberera Dzina la Yesu Khristu.

<sup>150</sup> Inu mukuti, “Ndine wa mpingo. Aleluya! Ulemelero kwa Mulungu! Ine . . .” Ndinu wa chiyani?

Mpingo ndi Mawu! Ndipo Mawu amati, “Ndi chamanyazi kwa inu kuchita zimenezo.”

Inu gulu la khungu la Afarisi, kuwatsogolera ana osauka amenewo ku gehena monga choncho; chifukwa inu mukuwopa chiphaso cha chakudya, ndipo angakuchotseni ku chipembedzo chanu ngati inu mungayambe chinachake chokhudza Iwo. Manyazi pa inu, achinyengo inu! Muchite nazo manyazi. Powona ora likuyandikira monga chonchi, ndipo inu mukutembenuka mwa miyambo yanu kuchoka ku Mawu a Mulungu. Mukuchitiranji, akhungu inu!

<sup>151</sup> Kodi Baibulo silimanena kuti munachititsidwa khungu? Kodi simukumvetsa kuti ndinu akhungu? Baibulo linati inu munali. “Ndipo inu ndi amaliseche, omvetsa chisoni, atsoka, akhungu, ndipo simukudziwa izo.” Pamene inu mukuganiza kuti muli ndi mpingo wawukulu kwambiri mu mzinda, ndipo inu mumachita *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*; ndipo Baibulo linati ndinu osauka momwe inu mungakhalire, ndipo ndinu akhungu. Ndipo Iye wayimabe pakhomo, akuyesera kuti akugulitseni inu mankhwala a mmaso; osati kugulitsa iwo kwa inu, koma kukupatsani inu, ndipo inu simukulandira iwo. Zikukwaniritsa Lemba.

<sup>152</sup> Kodi inu mukukhala tsiku lanji, anthu? Kodi inu mukulizindikira ora, mukuzindikira chizindikiro?

<sup>153</sup> Iwo akanangozindikira, akazi amenewo, kuti ameneyo ndi mdierekezi. Ndi mdierekezi wosayenera, mu dzina la chipembedzo. Iye wakhala ali choncho nthawizonse. Iye amabwera kwa mneneri aliyense, iye amabwera kwa wanzeru aliyense, iye amabwera ngakhale kwa Yesu Khristu, ngati munthu wachipembedzo. Ndipo Baibulo linati iye akanadzakhala “pafupi kwambiri m’masiku otsiriza,” ngakhale Achipentekoste, “ndipo akanadzanyenga osankhidwa omwe,” kuchokera mu mpingo wa Chipentekoste umenewo, “ngati kukanakhala kotheka.” [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

<sup>154</sup> “Apang’ono,” Iye anati, “chifukwa khwalala ndiro chipata ndipo njirayo ndi yopapatiza, ndipo koma ochepa adzakhalapo amene ati adzayipeze iyo. Pakuti monga kunali m’masiku a

Nowa, m'menemo anthu eyiti anapulumutsidwa, chomwechonso kudzakhala pa kudza kwa Mwana wa munthu." Taganizani za zimenezo! Kodi ife tikukhala mu tsiku lanji? Kodi inu mukulizindikira oralo, mukulizindikira tsikulo?

Ine ndikutenga nthawi yanu yambiri, koma ndiri ndi maminiti angapo owonjezera. Mukuona?

<sup>155</sup> Kuwapangitsa iwo kuti azimeta tsitsi lawo. "Chabwino," iwo amati, "mpingo wathu supereka chidwi ku izo." Inu mukudziwa chifukwa chake? Iwo ndi akhungu.

"Palibe vuto kudula tsitsi lanu." Baibulo limati liripo! Icho ndi chinthu chosayenera kwa inu ngakhale kumeta tsitsi lanu ndi kumapemphera.

Inu mukuti, "Chabwino, mkazi ayenera kuphimbidwa." Ndipo Baibulo linanena kuti "tsitsi" lake ndi chopimba chake. Osati chipewa; tsitsi lake!

<sup>156</sup> Nanga bwanji ngati Mose akanati, "Ine ndivula chipewa changa m'malo mwa nsapato zanga"? Izo sizikanagwira ntchito. Mulungu anati "nsapato," ndipo Mulungu amatanthauza nsapato.

Iye anati "tsitsi," osati chipewa! Ulemelero kwa Mulungu! Iye anakonda izo, ine ndikutsimikiza. Matamando akhale kwa Mulungu! Iye amatanthauza basi chomwe Iye wanena. Malemba alibe kutanthauzira kwa mseri. Samangotanthauza za chipembedzo chanu chokha; Iwo amangotanthauza zomwe Iwo akunena, ndipo Iye ndi wotanthauzira.

<sup>157</sup> Kutu, "Ine ndikumudziwa mkazi yemwe amachita izo." Ine sindikusamala zomwe inu mukudziwa. Ine ndikudziwa chimene Mulungu ananena pa izo. Inu muziyenere nokha.

<sup>158</sup> Ngati iwo akanangozindikira chomwe icho chiri, dona. Uh! Ngati inu mukanangozindikira! Kapena, "mkazi," osati dona.

<sup>159</sup> Ine ndinawona chizindikiro, ndikutsika kuchokera ku Blue Boar, ndikutsikabe, ine ndikukhulupirira ndi Fifth Street uko, malo ena ogulitsira mowa, anati, "Matebulo a madona." Ine ndinangoyima pamenepo; ine ndinati, "Inu simunakhalepo nawo amodzi." Dona sangapite kumalo oterewo. Mkazi akhoza, koma osati dona.

<sup>160</sup> Kodi inu munazindikira, kugwa kwa dziko kunayamba ndi nyansi za mkazi? Kodi inu mukudziwa kuti ilo lidzatha mwanjira yomweyo, nyansi za mkazi? Ndipo mpingo, umayimira, ndi mwa mkazi? Mpingo ndi mkazi, kuyankhula mwauzimu.

Chomwechonso Mkwatibwi ndi mkazi, kuyankhula mwauzimu.

<sup>161</sup> Kupanda makhalidwe kwa mpingo, momwe izo zimachitikira! Tayang'anani pa masomphenya, tayang'anani pa zinthu, taonani masomphenya ngakhale amene Mulungu

amapereka, ndipo masomphenya amenewo ndi owona. Ine ndiri ndi Baibulo langa pa mtima wanga, kwa anthu inu pa tepi; omvetsera akhoza kuziwona izo. Ine ndinaziwona izo! Mulungu Wamphamvuzonse akudziwa kuti izo ndi Choonadi. Sindinadziwepo mpaka pano. Ndi uyo apo, “amaliseche, ndipo osadziwa izo.” Iye amangokhala ndi nthawi yake yabwino. Ndi inu pamene.

Koma pamene Mkwatibwi wamng'onoyo anabwera powonekera, izo zinali zosiyana. “Alfa ndi Omega!” Uhuh.

<sup>162</sup> Mdierekezi amachita zimenezo. Koma monga Ayuda akale, pamene iwo awona Mawu . . .

Ndipo Yesu anati kwa Ake, Iye ananena izi kwa ophunzira Ake, “Fufuzani Malemba. Inu, inu mukudziwa, mukudabwa za Ine ndi utumiki Wanga. Fufuzani Malemba. Mwa Iwo inu mukuganiza kuti muli nawo Moyo Wamuyaya, ndipo Iwo amachitira umboni za Ine, Iwo amakuuzani inu chimene Uthenga Wanga uli. Ngati inu simungandikhulupirire Ine, khulupirani Mawu omwewo amene Mulungu akutanthauzira kwa inu.”

<sup>163</sup> “Ife sitikhala ndi Munthu uyu kuti azitilamulira ife. Ife tiri ndi ansembe athu omwe, ndi ena otero.” Pitirizani ndiye, ndizo zonse zomwe zinganenedwe. Nthawi yatha kwambiri, mulimonse. Mukuona? Miyambo yachipembedzo imene imati izo ndi zabwino, iwo amamvetsera kwa zimenezo. Iwo angakonde kumva . . . Inu mumakhulupirira a—mawu a—a munthu kuposa momwe mumakhulupirira Mawu a Mulungu. Iwo samazindikira. Mipingo masiku ano simazindikira Timoteo Wachiwiri 3. Ngati inu . . .

<sup>164</sup> Ine ndikuwona ena a inu mukulemba Malemba. Tsopano, awa ndi Malemba omwe ine ndikuwabwereza kuchokera pomwe apa. Pamene, ngati aliyense atachitika kuti atenge tcheru changa pa izo, kapena dzanja langa pa izo, ine ndikhoza kuwawonetsa iwo Lemba la izo. Mukuona?

<sup>165</sup> Iwo samazindikira Timoteo Wachiwiri 3, pamene Iwo anati, “Mmasiku otsiriza, anthu adzakhala aliwuma, odzikuza, okonda zosangalatsa kuposa okonda Mulungu, ophwanya malamulo, onenera zabodza, osadziletsa, ndipo onyozza iwo amene ali abwino (Mkwatibwi), mwaona; okhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma kumakana Mphamvu yakeyo; kwa oterowo chokaniko. Pakuti ili ndi gulu limene limapita nyumba ndi nyumba, ndi kuwatsogolera akazi opusa, akazi opusa, otsogozedwa ndi zilakolako za mitundu yosiyanasiyana, osaphunzira nkomwe kapena osatha konse kubwera ku chidziwitso cha Choonadi.” Osatero! Iwo sangachite zimenezo, ndipo iwo sangachite izo. Mulungu ananena chomwecho.

Ndipo, Mfarisi wakhungu, kodi iwe sukuziwona izo? Ine sindinakwiye; ndikungolondolera msomali ndi kuwukhomerera iwo. Ngakhalenso mipingo sikuzindikira Izi. Azimayi sangamvetse zimenezo. Iwo akuyenera... “Akazi opusa, otsogozedwa ndi zilakolako zosiyanasiyana,” Hollywood, mtundu wonse uwu wa zinthu, tsitsi lodula, kuvala akabudula, kuvala zodzoladzola, mtundu wonse uwu wa zinthu, zomwe ziri zosayenera. Kodi mukudziwa kuti mkazi amachita gawo lalikulu m’masiku otsiriza?

<sup>166</sup> Inu mukudziwa Baibulo linanena, kuti, “Iwo amene adzapulumuka ku chiwonongeko chachikulu ichi adzakhala nthambi yokongola pamaso pa Ambuye”? Tsiku lina ndidzafika ku zimenezo, Ambuye akalola, kwa izo, kwa inu akazi. Kudzakulonani inu kuti mudzawone chimene Mulungu amaganiza za mkazi amene wapulumuka kwenikweni chiwonongeko ichi cha tsiku lino. Anati, “Iye adzakhala wokongola.”

<sup>167</sup> Ine ndinamumva mkazi, tsiku lina, akumuseka... Mtsikana, gulu la akazi ovala mwatheka, okhala ndi makhalidwe otsika kuposa a—kuposa galu wamkazi, kumamuseka mayi wachikulire wovala diresi lalitali. Mvetserani apa, inu mkazi wamng’ono wokhotakhota iwe, iye ali ndi chinachake chimene iwe sukudziwa kanthu. Iye ali ndi makhalidwe. Iwe sukudziwa nkomwe chimene dzina lake liri. Iwe unataya izo mu chikuta, pafupifupi. Iwe sukudziwa nkomwe chabwino ndi choyipa; iye akudziwa. Iye ali ndi chinachake chobisika mu mtima mwake chimene iwe sukudziwa kanthu ka icho. Iwe unachitaya icho; sungachipeze icho. Iwe usati umutche iye wachikale, ndi zina zotero, monga choncho. Iye amadziwa chinachake chimene iwe sumadziwa kanthu ka icho. Iye wabisa mu mtima mwake, chuma cha khalidwe. Iwe sukudziwa liwu limodzi la izo. Amayi ako anakulela iwe monga choncho. Abusa ako analola izo; zikuwonetsera pamene iwo ayima. Ine ndikulalikira za iye pompano tsopano. Mukuona? Mukuona pamene inu muli, mipingo?

<sup>168</sup> Yesu anati, “Lemba lonseli likuyenera kukwaniritsidwa.” Ndipo Ilo lakwaniritsidwa.

<sup>169</sup> Zindikirani, “Monga Yane ndi Yambre nawonso anatsutsana ndi Mose,” iye adzabwera motsatira, ena a iwo. Osati, tsopano, iye sakuyankhula za Methodisti, Baptisti, apa; iwo ali kunja kwa chithunzicho. Mukuona? “Koma monga Yane ndi Yambre anatsutsana ndi Mose ndi Aroni, chomwechonso iwo adzatero; munthu wa malingaliro opotoka pa Choonadi,” atapotozedwa mu mbalume ndi ziphunzitso za mpingo, mmalo mwa Baibulo.

Ndipo kenako Yane ndi Yambre amatha kuchita chirichonse chimene Mose amatha kuchita. Mwaona, “monga Yambre,” mukuwona kufanana pamene?

“Monga Yane ndi Yambre anatsutsana ndi Mose, momwemonso amuna awa amalingaliro opotoka pa Choonadi, amachikana Icho,” sadzakhala ndi Iwo mwa oyandikana nawo, sadzagwirizana nkomwe ndi Iwo, sadzakhala ndi kanthu kochita ndi Iwo. Koma anati, “Kupusa kwawo kudzadziwika.” Pamene Mkwatibwi ameneyo adzatenga kuyima Kwake ndi kusunthira mmwamba mlengalenga, izo zidzadziwika, musadandaule; monga Mose, pamene iye anawatenga ana a Israeli, ndi kuthawa kuchoka Igupto, ndipo Igupto anamira. Chabwino.

<sup>170</sup> Yesu anati, “Malemba onse amaperekedwa mwa kudzodza, chomwechonso Malemba onse ayenera kukwaniritsidwa.” Pamene Iye . . .

Iwo anamufunsa Iye, anati, “Inu mumadzipanga Nokha Mulungu.”

<sup>171</sup> Iye anati, “Inu, mu chilamulo chanu, mumawatcha aneneri amenewo amene Mawu a Ambuye anabwera kwa iwo, inu munkawatcha iwo ‘amulungu,’ ndipo iwo ali.” Anati, “Ndiye inu munganditsutse bwanji Ine pamene Ine ndikuti Ine ndi Mwana wa Mulungu? Malemba onsewa amaperekedwa mwa kudzodza; onse a Iwo akuyenera kuwonetseredwa, onse a Iwo akuyenera kukwaniritsidwa.”

Mwaona pamene, iwo ndi akhungu kwambiri basi, iwo anali atatengeka kwambiri ndi mawu a munthu mmalo motengeka ndi Mawu a Mulungu. Icho ndi chimene chimapangitsa akazi kuchita zimenezo. Icho ndi chimene chimapangitsa alaliki kuchita zimenezo. Iwo amatengeka ndi bishopu mmalo mwa Yesu. Iwo amatengeka mu zimenezo, ndi lawo—ndi thumba lawo la ndalama, osonkhana aakulu.

<sup>172</sup> Mungowona ngati ine ndiri wotchuka. Mudzawatenge anthu, akunja kwa Jeffersonville, ndi gulu laling’ono lomwe liri kuno lochokera ku Jeffersonville; mudzawatenge akunja, aku Jeffersonville, mudzawachotse mkachisi uyu mmawa uno, ine sindidzakhala kapena kukhala ndi theka la thwelofu oti ndiwalaliki. Icho ndi chiyani? Iye ndi wopangidwa ndi konsekonse mdzikoli; kuchokera ku New York, kuchokera ku Massachusetts, ku Boston, Maine, Tennessee, Georgia, Alabama, ndi kuzungulira dzikoli. Iwo akusonkhana pamodzi. Ameni! Icho ndi chimene Iye ananena. “Kudzakhala Kuwala nthawi ya kumadzulo.”

<sup>173</sup> Iwo sangazindikire Kuwala kwa kumadzulo. Ndiro limene liri vuto. Iye basi sakuwazindikira Iwo. Iye ndi wakhungu kwambiri. Baibulo linati iye anali.

<sup>174</sup> Russia anangolandira malo ake mdziko, mu sayansi, osaposa zaka forte zapitazo. Inu mukudziwa, pamene Nkhondo Yadziko lonse Yoyamba inabwera, iwo sanati . . . Iwo anamsiya Russia. M’bale Roy . . . Ilo linali gulu chabe la mbuli, anthu achikulire aku Siberia, ndevu ziri pa nkhope pawo ponse, ndipo

sankadziwa dzanja lamanja ndi lamanzere. Uko nkulondola, Russia, koma iye anazindikira malo ake. Iye ankayenera kuti achite izo kuti akwaniritse Lemba. Inu mukudziwa mauneneri anga a zomwe ine ndinanena kuti zikanadzachitika, momwe iwo onse akanasonkhana mu chikominisi. Tsopano iye akutsogolera dziko mu sayansi. Ife tiri kumbuyo kwenikweni kwa iye. Ena onse a mdziko ali kumbuyo kwake. Iye akutsogolera malo ake. Iye anangozindikira kuti anali ndi ubongo, nayenso.

<sup>175</sup> Zindikirani, munthu ali ndi mphamvu sikisi zomwezo zomwe anali nazo zaka sikisi sauzande zapitazo. Zaka sisiki sauzande zapitazo, ndi mphamvu zomwe iye anali nazo, iye anafika kwawo kwa padziko lapansi ndipo anamutumikira Mulungu. Ndipo tsopano, mu zaka sevente-faivi zapitazo, munthu ameneyo wabwera kuchokera ku kavalo ndi ngolo, wapita ku wamu chombo. Chifukwa chiyani? Iye anachoka ku chikhulupiro chake mwa Mulungu, ndipo anachitembenezira ku mphamvu zake ndi kuthekera kwake ngati munthu. Kodi inu munazindikira izo? Iye anasiya kumdalira Mulungu. Amadzidalira yekha.

<sup>176</sup> Monga mkazi wosakhulupirira uyu. Dzina lake ndi ndani, Washington uko, yemwe anasintha zonsezi? [Wina akuti, “Murray.”—Mkonzi]. Kodi dzina lake ndi ndani? [“Murray.”] Murray, iye anati, “Bola ngati tiri ndi gulu lankhondo ndi apanyanja, sitikumusowa Yehova wokalamba.” Uh-huh. Ine sindikusamala chimene ife tiri nacho.

Ndi Yehova kapena palibe kanthu, kwa ine. Mulole asilikali ankhondo ndi apanyanja amile, ndipo izo zidzatero, koma Yehova adzakhalapo kwa nthawizonse. Bola ngati ine ndiri gawo la Iye, ndi mwana Wake, ine ndidzakhalabe ndi Iye kwanthawizonse; osati mwa maitanidwe anga kapena kusankha kwanga, koma mwa kusankha Kwake. Ameni, ameni! Analibe chochita ndi izo. Iye ndi Mmodziyo! Ndipatseni ine Iye kapena mundipatse imfa. Mulole mafuko adzuke ndi kugwa; Yehova adzakhalapobe. Iye wachita izo, monse kudutsa mibadwo; pamene Roma anagwa, pamene Igupto anagwa, ndipo ena onse a iwo anagwa. Ndipo Iye akadali Yehova. Oh, aleluya! Ine ndikumverera mwachipembedzo.

<sup>177</sup> Chifukwa chiyani Russia anabwera kwa iyemwini, ankayenera kutero. Chimodzimodzi monga momwe Israeli ankayenera kukalowa mu dziko la kwawo. Mulungu anachita kumusunthira Israeli kubwerera ku dziko la kwawo, chifukwa cha Malipenga. Ndipo chomwechonso Mulungu ayenera kumusunthira Russia kumtunda uko, mu chikominisi, kuti akachite ndendende zimene zinaloseredwa kuti iye akanadzachita.

<sup>178</sup> Munthu ndi mphamvu zake sikisi zinali zitangobwera kumene, kavalo ndi ngolo, akudalira Mulungu. Mu zaka sevente-

faizi zapitazi, iye anasiya kumudalira Mulungu. Pamene iwo anasayina malamulo a United States uyu, iwo anamuyika Mulungu mu chirichonse chimene iwo ankachita. Tsopano iwo alibe nkomwe msonkhano, ndipo samatchula nkomwe Dzina Lake. Uko nkulondola. Iwo amadalira pa kuzikweza kwawo kwa sayansi yawo, iwo, kuthyathyalika kwawo kwa sayansi yawo; gulu lachisembwere. Uko nkulondola ndendende. Dziko lonse lapansi lamezedwa ndi kusadziwa Baibulo. Ba- . . . dziko lonse lapatuka kwa Mulungu.

Koma, tangoganizani, pakati pomwe pa zonsezo, ndi zipembedzo za mpingo ndi chisembwere chawo chonse cha ku seminare ndi chirichonse, Mulungu wawatenga Mawu a aneneri Ake ndipo wamudula Mkwatibwi yemwe ati adzakhulupirire. Anati Iye akanadzachita izo. Iye wadula kuchokera ku chinthu icho chimene Iye analonjeza kuti Iye akanadzachita.

<sup>179</sup> Iwo amadalira luntha lawo la umunthu, sayansi yawo ya umunthu, ndi zina zotero; anamusiya Mulungu, Amene poyamba ankamudalira. United States yamusiya Mulungu kunjira. Iwo anamuthamangitsa Iye ngakhale ku sukulu, pakuti ana athu aang'ono sangathe nkomwe kumva za Iye. Iwo anamutulutsa Iye ku sukulu. Tsopano iwo akuyesetsa kuti amuchotse Iye pa madola, "Mwa Mulungu ife timadalira." Iwo achotsa izo pa lonjezo la kukhulupirika ku mbendera, "Fuko limodzi pansi pa Mulungu." Iwo azichotsapo izo.

<sup>180</sup> Mwaona, iwo apita ku zomverera zawo zomwe ndi zokhudzira zawo zomwe. Chifukwa, mu zaka sevente-faivi zapitazi, iye sanasinthe pang'ono mu zokhudzira zake, iye akadali munthu yemweyo amene Mulungu anamulenga iye pachiyambi.

Koma, mmasiku otsiriza ano, kodi inu simungazindikire pamene ife tiri? Ndipo mpingo watembenuka, wachoka kwa Mulungu, wapita ku zimenezo, wapita ku seminare ndi chokuchitikira, ndi zina zotero, mmalo mwa Mawu. Sakumuzindikira Iye nkomwe mmisonkhano yawo, mmasukulu awo, kapena kalikonse, panonso.

<sup>181</sup> Israeli, mu zaka twente-faivi zapitazi, wazindikira kuti chinachake chawabweretsa iwo ku dziko la kwawo, monga zinalonjezedwa. Iwo sakudziwa momwe izo zinachitikira. Iwo anavutika monga chirichonse, kufera, pansi pa Malipenga amenewo, koma iwo ali mdziko la kwawo. Iwo sakudziwa chifukwa chake.

<sup>182</sup> Nchifukwa chiyani Russia inadzuka? Nchifukwa chiyani mafuko anadzuka? Nchifukwa chiyani munthu wakwanitsa kuchita bwino? Pamene asayansi, zaka firii handiredede zapitazo, wasayansi waku France anagudubuzwa mpira pa liwiro linalake padziko lapansi, ndipo anatsimikizira, ndi kafukufuku wa sayansi, "Ngati munthu atapanga konse liwiro lowopsya la

mamailosi sarte pa ora, mphamvu yokokera pansi ingamuchotse iye pa dziko lapansi; mogwirizana ndi kulemera kwake, mogwirizana ndi kulemera kwa mpirawo.” Tsopano iye akupita mailosi seventini sauzande pa ora, mwaona, akuyesetsabe kuti azikwera. Iye wangozindikira kumene zimenezo, posachedwapa. Chifukwa chiyani? Zikuyenera kukhala mwanjira imeneyo.

<sup>183</sup> Bwanji, mpingo unkayima pa thanthwe la Yesu Khristu. Ziribe kanthu zomwe aliyense ankanena, iwo ankakhalabe ndi Mawu amenewo, uthenga wa ora; Luther, Wesley, ndi kumatsika kudutsa kumeneko. Ndipo tsopano iwo abwerera ku miyambo. Nchifukwa chiyani iwo wachita zimenezo?

<sup>184</sup> Zaka twente-faivi zapitazo, Israeli wangozindikira kumene kuti ali mdziko lakwawo chifukwa cha chinachake. Izo zinaloseredwa kuti adzasonkhanitsidwanso kachiwiri; Hoseya ananena zimenezo. Iye tinaziwerenga izo kanthawi kapitako. Mulungu atithandize ife kuti timvetse zimenezo! Chabwino.

<sup>185</sup> Pa nthawi yomweyo, Mkwatibwi wazindikira Kuwala kwa kumadzulo, wangoyamba kuzindikira. Achipentekoste anjala ayamba kuzindikira kuti mabungwe amenewo alibe zinthu zirizonse zomwe iwo amazifuna, iwo apotozedwa kwambiri ndi kung’ambidwa. Mwaona, ndi nthawi ya kuzindikira, kuzindikira. Inu muyenera kuti muzindikire.

Dziko lazindikira. Mafuko azindikira. Sayansi yazindikira. Mdirekezi wazindikira kuti ndi nthawi yomwe iye akhoza kusokoneza akazi, kuwusokoneza mpingo, kuwasokoneza anthu. Iye wazindikira zimenezo.

Ndipo Mulungu wazindikira kuti pali anthu pa dziko lapansi amene Iye anawakonzeratu ku Moyo. Iye anazindikira kuti iyi ndi nthawi yoti atumize Uthenga Wake. Iye wachita izo. Anthu awuzindikira Iwo, nthawi ya Mkwatibwi yazindikira Kuwala kwa kumadzulo.

<sup>186</sup> Ngati Sodomu akanazindikira masiku ake, pamene iye anawona atumiki amenewo akubwera kumusi uko, monga Billy Graham ndi Oral Roberts!

<sup>187</sup> Tsopano, munthu wina wachisembwere mu Phoenix anangoyimirira ndi kunena... anasewera gawo limenelo pa—tepi, ndipo ananena kuti ine ndinanena kuno, ine “ayenera kubatizidwa mu Dzina la Yesu,” ndinanena zimenezo. Ndipo kenako anati, “Tsopano inu mwaona *apa*, cha apa iye anati. . .” Pamene ndinkayankhula za Afrika, momwe iwo amabatizira katatu chogwetsegera nkhope mtsogolo, ndi kumbuyo. Anati ine ndinati, “Sizimapanga kusiyana kulikonse.” Mwaona, iye sanasewere konse tepi yonseyo; gawo lokhalo basi, nkudzaidula iyo.

Chimene, chingakhale mlandu waku ndende kuchita izo. Matepi amenewo mwamtheradi ali ndi umwini. Palibe amene angawasokoneze iwo. Inu kulibwino musatero. Inu—inu—inu



muli ndi lamulo pa inu. Koma kodi ife tingachite zimenezo? Ayi. Iye anati, “Asiyeni iwo okha.” Mulungu anandiuzza ine chimene chiti chidzachitike. Mungopenya, mungoyika diso lanu pa munthu ameneyo. Mukuona?

<sup>188</sup> Nthawi yomweyo, Mkwatibwi wazindikira Kuwala kwa kumadzulo.

Ngati Sodomu akanalizindikira ora lawo!

<sup>189</sup> Tsopano, munthu yemweyu anayika tepi, anati, “Taonani apa, kwa inu anthu Achipentekoste,” anati, “ndi inu Abaptisti. Munthu uyu, mneneri wabodza, William Branham,” mwaona, “wanena kuti Oral Roberts ndi Billy Graham anali ku Sodomu.” Mwaona, kenako nkuidula tepiyo; ndizo zonse, mwaona.

Sanapitirire patsogolo kukanena, kuti, “Iwo anali amthenga ku Sodomu.” Osati ku Sodomu, “Iwo anali kumeneko ngati wa mthenga ku Sodomu.” Aliyense akudziwa kuti ine ndinanena zimenezo. Kasewereni tepi yanuyo.

“Aliyense amene adzachotsapo kapena kuwonjezerapo, zomwezo zidzachotsedwa kwa iye.” Ndi Mawu a Ambuye. Iwo amayima mwanjira imeneyo.

<sup>190</sup> “Ngati Sodomu akanazindikira wa mthenga wake, iye bwenzi akuima lero,” Yesu anati, ngati iye akanazindikira chimodzimidzi monga Abrahamu anazindikira.

Abrahamu ankadziwa kuti panali mwana wolonjezedwa akubwera. Koma iye ankadziwa kuti pankayenera kukhala kusintha mwanjira yina, chifukwa iye anali wokalamba kwambiri, ndipo chimodzimidzinso ndi Sarah. Koma pamene iye anamuwona Mmodzi uja Amene amakhoza kuzindikira malingaliro a Sarah, kumbuyo kwa Iye, iye analizindikira ora limene iye ankakhalamo. Iye anati, “Ambuye wanga, mundirole ine nditenge madzi pang’ono pano ndipo ndisambitse mapazi Anu.” Iwo anadya chidutswa cha mkate. “Ndiroleni ine ndikupempheni Inu, dikirani pang’ono pokha,” onani, apa, “A-m-b-u-y-e wanga,” chilemba chachikulu A-m-b-u-y-e, “Elohim.” Iye anazindikira kuti Mulungu ankayankhula kwa iye kuchokera mu mnofu wa munthu. Iye anazindikira chizindikiro chake, ndipo anadalitsidwa ndi Ambuye.

Sodomu sanazindikire tsiku lawo, ndipo anawotchedwa. Yesu anati, “Monga izo zinali mu tsiku limenelo, chomwecho izo zidzakhala pamene Mwana wa Mulungu ali . . . kapena Mwana wa munthu azidzawonetseredwa.”

<sup>191</sup> Tsopano, mpingo sunazindikire tsiku lake. Monga Israeli, anakakamizika kubwerera ku Palestina, iye akakamizidwira mu Bungwe la Mpingo ya Mdziko. Chifukwa chiyani? Iye sanazindikire ora lake. “Anthu, tulukani mwa iye, musakhale otenga nawo gawo la tchimo lake!” Thawitsani, moyo wanu,

kapena inu mudzagwidwa ndi chilemba cha chirombo ndipo simudzachita china chirichonse ndi izo.

“Msiyeni iye amene ali woyipa akhale chiyipire. Msiyeni iye amene ali woyera,” osati *adzakhala* woyera, “woyera tsopano. Msiyeni iye amene ali woyera,” osati bab-...mkazi wodula tsitsi; iye sangakhale. Tsopano, izo zikumveka mosapysatira, koma limenelo ndi Lemba. Baibulo limati, “Iye amanyozetsa mutu wake,” ndipo mutu wake ndi mwamuna wake. Mutu wa mwamuna ndi Khristu, chotero mkaziyo amanyozetsa Khristu. Iye angakhale bwanji “wosalemekezeka” ndipo osakhala “wonyansa”? “Muloleni iye amene ali ndi tsitsi lodulidwa alisunge ilo. Muloleni iye, iye amene amavala akabudula azivala iwo. Muloleni iye amene amakana Mawu apitirize kuwakana Iwo.”

“Koma iye amene ali woyera akhalebe woyera. Iye amene ali wolungama akhalebe wolungama; Mawu olungama a Mulungu, Mwana wa Mulungu akuwonetseredwa. Khalanibe woyera, akhalebe wolungama!” Zindikirani! Inde, bwana! Masiku osati. . .

Mpingo sunalizindikire tsiku lake.

<sup>192</sup> Monga Israeli, wabwerera mdziko lake lolonjeredwa, iye sakudziwa momwe iye anabwererera kumeneko. Iye anangokaikidwa kumeneko mosadziwa. Bwanji? Mphamvu ya fuko inakamuika iye kumalo ake.

Tsopano ine ndinena chinachake. Mphamvu ya fuko inakamuika Israeli mdziko lakwawo; mphamvu ya fuko inakamuika mpingo mu Bungwe la Mipingo ya Mdziko; koma mphamvu ya Mulungu idzawayika anthu mwa Mkwatibwi. Dziko limakankhira mbali *iyi*, ndipo dziko limakankhira mbali *iyi*, koma Mulungu amakankhira mmwamba. Mzimu wa Mulungu, umene uli Mawu a Mulungu, “Mawu Anga ndi Mzimu ndi Moyo,” udzayika Mkwatibwi mmalo Ake. Chifukwa, Iye adzawazindikira malo Ake mu Mawu, ndiye Iye ali mwa Khristu, adzamuyika Iye mmalo Ake. Palibe mphamvu ya fuko imene idzachite zimenezo. Koma mphamvu ya fuko inathamangitsira Israeli kupita ku dziko lakwawo; mphamvu za fuko la Bungwe la Mipingo zidzathamangitsira bungwe lililonse mmenemo; koma Mphamvu ya Mulungu idzamuwukitsira Mkwatibwi kukalowa mu Ulemelero, kuchoka mmenemo.

<sup>193</sup> Oh, anthu, zindikirani tsiku lanu, monga Yesu anakuchenjezerani inu; chizindikiro cha Sodomu, ndi zikhalidwe za mpingo wa tsiku lino.

<sup>194</sup> Penyani zomwe Iye ananena mu tsiku lino zimene zikanati zidzachitike. Mvetserani kwa izo mwatcheru kwenikweni. Chizindikiro cha Sodomu chidzachitika mu tsikuli; chizindikiro monga Abrahamu, tsiku lija pamaso pa Sodomu, yemwe anatulutsidwa. Zinthu zonsezi zimene

zinaloseredwa, zidzakhala zikuchitika tsopano. Penyani tsiku lomwe mukukhalamo. Ife tapita pamwamba pa ilo ndi pamwamba pa ilo.

<sup>195</sup> Tsopano Iye walonjeza kuti akutumizirani inu Kuwala kwa Kumwamba, kuti kukachetse Mbewu ya Mawu yomwe iti idzafesedwere tsiku lino. Mbewu ili *Muno*. Mbewuyo ndi Baibulo. Chifukwa chiyani? Yesu ananena chomwecho. “Mawu ndi Mbewu imene wofesa anafesa.”

Ndipo, tsopano, musanakolole mbewu iliyonse, ziribe kanthu ngati mutafesa mbewu, iyo imayenera kukhala ndi kuwala kuti kuichetse mbewu imeneyo, kapena iyo idzavunda ndipo siidzachita ubwino uliwonse; iyo idzawonongeka. Koma ngati iyo ili ndi mbewu mu nthaka, nthaka yoyenera, ndi mtundu woyenera wa kuwala kwa dzuwa pa iyo, iyo idzayenera kucha.

Ndipo Iye analonjeza kuti mmasiku otsiriza, mu nthawi ya kumadzulo, Mwana adzatulukira kuti adzachetse Mbewu imeneyo. Mbewu ikulalikiidwa. Mwana wa Mulungu akuchetsa Mbewu imeneyo, poitsimikizira Iyo, kuyipangitsa Iyo kuti izikankhira kunja pamaso panu ndi kutsimikizira kuti Iyo ndi yolondola. Kodi mukumvetsa zimenezo? Lizindikireni tsiku lanu.

Ine ndikutseka tsopano. Ndi nthawi tsopano yoti nditseke.

<sup>196</sup> Ndipo Achilaodikaya olemera, akhungu, ophunzira adzawachotsa Mawu pakati pawo. Kodi iwo achita zimenezo? Iye anati iwo akanadzatero.

Monga aneneri akale anatumidwa kuti adzatsimikizire Mawu olonjezedwa a tsiku lawo, kotero kuti anthu amene anakonzedweratu, tsiku lawo, anawawona Iwo. Monga mkazi wa pa chitsime, monga Natani, monga Bartimeyo wakhungu, monga Petro, ndi ena onse a iwo amene anawazindikira Iwo. Iye anali Mawu amenawo. Ndipo kupukusa, “Ngati Ine sindichita ntchito zimene Atate analonjeza kuti Ine ndidzazichita, ndiye musandikhulupirire Ine. Koma ngati Ine ndikuchita ntchitozo, ngakhale simundikhulupirira Ine, mukhulupirire ntchitozo. Izo zimakuuzani inu Yemwe Ine ndiri.” Mukumvetsa zimenezo? Chabwino, musaliphonye tsikulo, lotumizidwa. Amuna ndi akazi a masiku enawo anawazindikira Iwo, ndipo anakalowa mkati ndipo anali otetezeka.

<sup>197</sup> Achipentekoste, oh, mai, bwanji inu simukulizindikira tsiku lanu? Lizindikireni tsiku la nthawi ya kumadzulo. Ilo liri pano, ndipo ilo liri pano, kuti, kudzatsimikizira kudza kwa Khristu, kudzatsimikizira izo. Ife tiri kumapeto. Lizindikireni tsiku lanu.

<sup>198</sup> Ine ndikudziwa kuti ndakusungani inu nthawi yayitali. Ndi thwelofu koloko tsopano. Koma, ndimachikonda Chakudya ichi, Ichi ndi Moyo. Icho chiri. Icho chiri, kwa wokhulupirira.

Lizindikireni tsiku lomwe mukukhalamo, ndi chizindikiro cha nthawi.

<sup>199</sup> Muwone pamene chirichonse chiri: Israeli; kumene mpingo; kumene chivundi; kumene Mkwatibwi wayima. Chatsalira ndi chiyani? Chinthu chotsatira, kutengedwera mmwamba kwa Mkwatibwi. Zoono, mpingo uliwonse ukuyembekezera chinthu chachikulu. Apentekoste amati, “Ulemelero kwa Mulungu! Lidzafika tsiku limene iwo ati adzachite *ichi*, ndipo iwo adzachita *icho*.” Mwaona, iwo ndi odzinenera. Iwo akukhulupirira.

<sup>200</sup> Monga, nthawi ina, Kayafa anati, “Kodi sikoyenera kuti munthu mmodzi afe, ndipo osati mtundu wonse uwonongeke?” Iye anali wansembe wamkulu, Baibulo linati, chifukwa chimene iye ananena zimenezo. Iye ananenera, asakudziwa chimene iye ankanena. Koma kodi iye anazindikira choonadi chenicheni cha izo, kuti iye ankamupereka Mulungu yemweyo amene iye ankadzinenera kukhala wansembe wamkulu wake?

Momwemonso izo ziri, lero! Iwo akuyembekezera, uko kwina kwake, kuti—nthawi yopambana ibwera.

<sup>201</sup> Bwanji, ine ndimapita mu msonkhano waukulu wa Amuna Amalonda ndi iwo. Iwo amati, “Ulemelero kwa Mulungu!” Alaliki amenewo amadzuka ndi kungokondoweza gululo, ndi kumati, “Kukubwera chitsitsimutso chachikulu. Dzanja la Ambuye lidzakhala pa dziko lapansi!” Ndipo momwe anthu akupitira patsogolo, akuthamanga monga... Ndipo sakuzindikira kuti zimenezo ziri pansu pa Malipenga a Israeli. Nchifukwa chiyani iwo akuchita zimenezo? Ndi chifukwa chakuti iwo ndi odzinenera Chikhristu, ndipo sakuzindikira. Ngakhalenso Kayafa sanazindikire zimene iye ankachita. Ndipo iwo sakuzindikira kuti iwo akuwukana Uthenga womwewo umene watumizidwa kwa iwo. Amen!

<sup>202</sup> Gawo lililonse la Lemba, tadutsa tsiku ndi tsiku, ndipo sabata ndi sabata, mpaka icho mosatsutsa ndi Choonadi. “Ngati akhungu sangalandire Iwo,” Yesu anati, “asiyeni iwo. Ngati wakhungu atsogolera wakhungu, onse amagwera m’mbuna.” Ine sindikudziwa ndi liti, sindikudziwa ndi kuti, koma ndikudziwa kuti zikubwera.

<sup>203</sup> Inu mukudziwa, ndikuwona chifukwa chimene Satana sanafune kuti ine ndichite ichi. Dzulo, ndinamverera moyipa kwambiri. Ine sindinathe kupeza Mawu aliwonse kuchokera kwa Ambuye. Ine ndinachita zonse zomwe ndimazidziwa, ndipo sindinathe. Ndipo mmawa uno, pamene ine ndimadzuka... Ine ndinadya chimanga, dzulo, ndipo izo zimawoneka ngati nditagona pamenepo mmimba mwanga. Ine ndinadwala kwambiri, ine basi—ine sindinathe kuzimvetisa izo. Ine ndinaganiza, “Kodi vuto ndi chiyani mdzikoli? Ine ndikupita kumeneko, ndipo ine sindikudziwa chimene ine nditi ndikanene.

Ndipo, Ambuye, ine ndikulephera ngakhale kuti ndipeze Lemba mmalingaliro anga, kuti ndilembe. Ine sindikuchipeza chinthucho.” Ine sindimadziwa basi choti ndichite.

Ndiye, Uthengawo utangoyamba kubwera kwa ine, Satana anapitiriza kumanena, “Ukumverera moyipa kwambiri. Mutu wako ukupweteka. Iwe ukudwala. Iwe sungapite kumusi uko. Iwe sungakaima kumeneko. Izo ziyenera kukhala *ichi*, zikakhala *icho*.”

<sup>204</sup> Ine ndikukumbukira, nthawi ina, nkhani ya munthu wamng’ono ku England. Iye anali munthu wamba chabe. Ndipo iwo ananena kuti a—a—mfumu, imodzi mwa mafumu m’masiku oyambirira ankalowa mu yake—nyumba yake yachifumu. Ndipo, uyu, iye analibe aliyense...Iye anali ndi uthenga womwe iye ankayenera kuti awupereke, uthenga wofunika, chifukwa cha mdani. Ndipo chotero iye—iye—iye anati kwa mwamuna wamng’ono uyu atayima pamenepo, iye anati, “Apa, utenge uthenga uwu, utenge uthenga uwu! Ufulumire nawo ku *enaake—enaake*, ndipo ukalamulire kuti *ichi* chikachitidwe.” Ndipo iye anati, “Utenge ndodo yanga m’dzanja lako. Imeneyo ikakutsimikizira iwe, kuti ine ndi...watumizidwa kuchokera kwa ine.”

<sup>205</sup> Ndipo iye anaiyika iyo pansa pa mwinjiro wake, ndipo iye anapita. Alonda paliponse akumuyimitsa iye, wina aliyense. Akufuula, “Chokanipo! Ndiri ndi uthenga wa amfumu.” Amen. “Ndine wa mthenga wa mfumu,” mawu otsimikiziridwa.

<sup>206</sup> Ine ndinaganiza, “Satana, choka panjira yanga! Ine ndiri ndi Uthenga wa Mfumu. Ine ndiyenera ndizipita.”

<sup>207</sup> Nthawi ina pamene iwo anamupha Kalonga wa Mtendere, ndi kumuyika Iye mmanda, ndipo anasindikiza mandawo, ndipo imfa inamugwira Iye kwa masiku atatu ndi usiku. Koma mmawa wa Isitara Iye anali ndi ndodo yachifumu mdzanja Lake, ndipo anafuula, “Chokako, imfa! Chokako, manda! Tsegula! Ndine Uthenga wa Mfumu. Ine ndiyenera kuti ndibwere kudzatsimikizira chiwukitsiro ichi. Ndine chiwukitsiro ndi Moyo.” Aleluya! Ine ndikumverera bwino kwenikweni tsopano.

Ndi Uthenga wa Mfumu. Tiyeni tiwuzindikire Iwo, abwenzi, pakuti ife tayitanidwa kuti tidzasonkhane pamodzi ku kuwomba kwa Lipenga. “Pakuti Lipenga la Ambuye lidzawomba, ndiye sipadzakhalanso nthawi.”

<sup>208</sup> Iye anasonkhanitsa Israeli. Masiku atatu, mu tsiku lachitatu Iye anati Iye akanadzachita izo. Zaka twente-seveni handiredede zadutsa. Mu tsiku lachitatu limenelo Iye anati Iye akanadzawasonkhanitsa iwo pamodzi, ndipo Iye wachita zimenezozo. Iye anati Iye akanadzadziwitsa njira ya Moyo. Ndi zimenezotu pamenepo, akungoyembekezera tsopano kuti Mkwatibwi achoke pa njirayo kuti iwo abwere, aneneri awiriwo, Aneneri Achihebrei, amene adzazindikira.

209 Inu mukundikumbukira ine nditayima ku Cairo, kuti ndizipita kumeneko, pamene Lewi Pethrus anati, “M’bale Branham, ngati iwo adzawone konse izo . . . Iwo amakhulupirira aneneri awo.”

210 Ine ndinati, “Ndicho chinthu chabwino kwa ine.” Mukuona momwe munthu amakhalira? Koma mukuona chisomo cha Mulungu? Ine ndinati, “Ndikawerenga Chipangano Chatsopano ichi.” Iwo amawerenga Icho. Lewi anawatumizira iwo, oposa milioni, kumeneko, M’bale Lewi Pethrus wochokera ku Sweden. Iwo amakhoza kuwawerenga Iwo, akubwera chokwera ndi chotsika kumeneko, Ayuda amenewo; osati monga gulu lamakono ili la Ayuda, koma mdziko la kwawo. Ndipo akubwera, iye anati, “Ngati uyu ali Mesiya, tiyeni ife timuwone iye akuchita chizindikiro cha mneneri, ife tikhulupirira izo.”

211 Lewi Pethrus anati, “M’bale Branham, ndi umenewo mwayiwo. Ndi umenewo mwayiwo.” Winawake anandiuza ine kuti—kuti iwo ukakhala mwayi. Ine ndinalondola, basi mpaka kwa izo.

Munthu wina anabwera ndipo anakhala pamenepo, M’bale Arganbright, anati, “M’bale Branham, izo zikangodzidzimutsa Israeli! Zikawabweretsa iwo pamaso pa Iwo, ndi kuwonetsera chizindikiro cha mneneri. Iwo akakhulupirira zimenezo.”

212 Ine ndinati, “Ambuye, ndine pano, ndakonzeka.” Ndinalumphira mu ndege; ndinatenga ndalama ndipo ndinagula tikiti; ndinayima ku Cairo. Ndinati, “Eya, ndakonzeka.”

213 Mzimu Woyera unati, “Awa si malo ako. Nthawi yake si ino.” Mwaona, iwe umapita patsogolo pa iwe mwini. Ine ndinaganiza, “Oh, mai! Ine ndabwera kuno; ine—ine ndikupita.”

214 Chinachake chinati, “Ima pomwe pano! Iwe usapite njira imeneyo. Utembukire ku India. Usapite kumeneko. Upite ku India, koma iwe usapite kuno.”

215 Ndinaganiza, “Chifukwa chiyani?” Pamene ndimatuluka kuseri kwa nyumba, ine ndinati, “Ambuye Yesu, izi zikutanthauza chiyani?”

Kenako Iye anandidziwitsa ine. “Palibe Wamitundu. Aneneri awa ndi amenewo.” Izo zikuyenera kukhala mogwirizana ndi Lemba. “Mose ndi Eliya akuyenera kubwera.” Ndipo, komanso, Mkwatibwi sanachotsedwebe pa njirapo. “Ndipo aneneri amenewo adzabwerera ndipo iwo adzachita chizindikiro cha mneneri.” Limenelo ndi Lemba. Kumeneko zonse zikukwaniritsidwa ndiye, mwangwiwo, Israeli ngati fuko adzabadwa mu tsiku limodzi. Amen! Kuwala kwa kumadzulo kukuwala!

Kudzakhala Kuwala nthawi ya kumadzulo,  
Njira ya Ulemelero ndithudi mudzaipeza;  
Mu njira ya madzi, muli Kuwala lero,

Kuyikidwa mmanda mu Dzina lofunika la Yesu.

Ana ndi akulu, lapani machimo anu onse,  
Mzimu Woyera ndithudi udzalowa;  
Kuwala kwa kumadzulo kwabwera,  
Ndi zoonza kuti Mulungu ndi Khristu ndi Mmodzi.

<sup>216</sup> Ife tiri pa nthawi ya kumapeto, mzanga. Ndiyeno ife tikuganiza za nyimbo iyi ya wolemba wodzodzedwa, pamene iye anati:

Mafuko akusweka: (Izi ndi pafupifupi zaka fifitini zapitazo.) Israeli akuwuka,  
Zizindikiro zimene aneneri ananeneratu;  
Masiku a Amitundu akwanira, (Tayang'anani pa nyansi zake tsopano.) ndi zowopsya zochulukana;

“Bwererani, O omwazikana, kwanu.”

Tsiku la chiwombolo layandikira,  
Mitima ya anthu ikulephera chifukwa cha mantha;

Dzazidwani ndi Mzimu wa Mulungu, mukonze nyali zanu ndipo ziziwala,  
Yang'anani! Chiwombolo chanu chayandikira.  
(Uko nkulondola.)

Aneneri abodza akunama, Choonadi cha Mulungu akuchikana, (Kodi izo si zoonza?)  
Yesu Khristu ndiye Mulungu wathu.

Iwo samakhulupirira Zimenezo. Iwo ali nayo mitundu yonse yama ism ndi zinthu! . . . ? . . . zoonza. Koma mneneri anati, kapena, wolemba wodzodzedwayo anati:

Tidzayenda pamene atumwi anaponda.

<sup>217</sup> Mukukumbukira mmasomphenya anga? Ine ndinati, “Ngati anthu a Paulo adzalowe, chomwechonso anga adzatero, chifukwa ine ndachita chimodzimidzi basi monga iye anachitira.” Ine ndikukhala ndi Iwo.

Mamillioni amenewo anaponyera manja awo, akuti, “Ife tikupumula pa zimenezo!”

Chiyani? Kulizindikira tsiku lomwe ife tikukhalamo, nthawi yomwe ife tikukhalamo, chizindikiro cha nthawi imene ife tikukhalamo. Zikhoza kukhala mochedwa kuposa momwe tikuganizira. Limodzi la masiku awa, mulole iye amene ali kunja akhalebe kunja. Iye amene ali mkati akuyenera kukhalabe mkati kwanthawizonse. Chitseko chitsekedwa.

<sup>218</sup> Ngati alipo ena pano mmawa uno amene sanalowepobe, oh, mu Dzina la Yesu, anthu anga okonedwa . . .

Musayang'ane pa wantchito mbuli uyu wayima apa, wosatha kuwenga, wosaphunzira, wosaphunzira; musayang'ane pa izo. Koma muyang'ane pa Mawu amene atsimikiziridwa. Muyang'ane pa Mzimu Woyera wawukulu Umene umatsimikizira Iwo kuti ndi Choonadi. Ife tiri mu nthawi ya kumadzulo. Ndi mochedwa kuposa momwe inu mukuganizira. Musati . . .

<sup>219</sup> Azimayi, mulole tsitsi lanu likule. Mlongo, chonde vulani zovala zonyansa zimenezo. Mutaire kutali ndudu zimenezo. Pakuti ora lidzafika, limene, “Iye amene ali woyipa, msiyeni iye akhalebe chiyipire; ndipo iye amene ali wolungama, msiyeni iye akhalebe wolungama. Iye amene ali mkati ali mkati; iye amene ali ku kunja ali kunja.” Malire aang'ono, apafupi, “Ngati munthu wolungama adzapulumutsidwe mosowa, wochimwa ndi wosapembedza adzakakhala kuti,” wokaka-Choonadi, inu mukudziwa, “kodi iwo adzawonekera pati?”

Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

<sup>220</sup> Tsopano, mu Kuwala kwa ora lino limene ife tikukhalamo tsopano, Kuwala kwa tsiku limene ife tikukhalamo tsopano; ofunika ndi okonedwa, inu amene mumachokera ku madera osiyanasiyana m'dziko lonselo, tiyeni tsopano, ndipo ine ndi inu, pa guwa ili, tiyeni tipange kufufuza. Kodi Mzimu wa Mulungu uli bwanji m'mitima mwathu lero? Kumbukirani, ndi Mzimu umenewo, wosayipitsidwa, wosayipitsidwa; chiphunzitso cha mpingo chirichonse, ndi chirichonse, chapita kwathunthu.

<sup>221</sup> Inu simungayerekeze kuyesa kuwonjezera kwa Iwo kapena kuchotsera kwa Iwo. Pakuti, ngati inu mudzayesera kuyika kutanthauzira pa Iwo, inueni, gawo lanu lidzachotsedwa mu Bukhu la Moyo. Kodi inu mukuyesera kunena chinachake chimene Mzimu sunanene? Kodi inu mukuyesera kuwapangitsa Iwo kumveka ngati Iwo ananena chinachake? Kapena, inu mukungowatenga Iwo ndendende zomwe Iwo ananena, ndi kuwasiya Iwo monga choncho? Kodi mukuphatikiza, mukudula, mukujambula, mukuchita zinthu zomwe ziri zosayenera? Inu mukutero?

<sup>222</sup> Nenani, “Chabwino, ine sindikumverera ngati ndikuyenera kuchita *ichi*. Kapena, mwinamwake, ine—ine—ine ndikudziwa mpingo wanga sumakhulupirira Iwo. ‘Amenewo ndi mawu a munthu mmodzi chabe pa Iwo.’”

Munthu mmodzi ameneyo ndi Mulungu. Baibulo apa limati musamete tsitsi lanu. Izi . . . Baibulo linanena zimenezo. “Zidzachitika kuti akazi azidzavala zovala ngati mwamuna, ndipo momwe iwo adzakhale chonyansa kwa Mulungu.” Momwe Mzimu Woyera unalankhulira kudzera icho, chotengera chonyozeka ichi, chosayenera chomwe chinangochitika kuti chiripo mu m'badwo umene Mfumu yaikulu inanena, “Apa pali manda Anga, Mawu Anga.” (“Nayi Ndodo Yanga yachifumu,”



kani.) “Utenge Ndodo Yanga, ndipo uzipita, ndipo ukabweretse Uthengawo.”

<sup>223</sup> Ndikudziwa zipembedzo zinayesera kuti ziwuletse Iwo, ndi kuwutulutsa Iwo, ndi kuwupondereza Iwo, ndi kuwumenyera Iwo, ndi chirichonse. Koma, mwa chisomo cha Mulungu, ndiri panjira yanga, ndikufuula kwa fuko ndi fuko, malo ndi malo, mpingo ndi mpingo, “Tulukani mu zimenezo!” Izo ndi zosatchuka, koma Iwo ndi Choonadi.

<sup>224</sup> Kodi inu muwalandira Iwo mu—mu—Mzimu umene Iwo analembedweramo? Kodi inu muwalandira Iwo mu Mzimu umene Iwo waperekedwamo? Ngati mukadali opanda panobe... Ife tiribe malo a guwa; mtima wanu ndiro guwa. Kodi mungakwezere dzanja lanu mmwamba, kuti, “Mulungu, mundichitire ine chifundo. Mulole Mzimu wa Mulungu ubwere mwa ine, unditsutse ine tsopano za machimo anga onse, ndi zokhumudwitsa, zizolowezi zanga zonse zoyipa, ndi kupsya mtima, ndi mikangano, ndi ndewu, ndi kudyana, ndi chirichonse chimene ine ndakhala nacho. Ndipo ine ndikudziwa chinachake, kuti mzimu wanga si wofatsa kwa Kumwamba. Ndi pangeni ine ndikhale wofatsa, Ambuye, mu mphindi yotsiriza iyi. Uwu ukhoza kukhala ulaliki womaliza umene ndidzawumve. Iyi ikhoza kukhala nthawi yotsiriza imene nditi ndidzamve Uthenga. Ine ndikukweza dzanja langa. Mulungu, mundichitire ine chifundo.”

<sup>225</sup> Mulungu akudalitseni inu. Manja ambiri. Tsopano, kwa mphindi yokha ya pemphero lachete kwa inu. Inu amene mwakweza dzanja lanu, mukusonyeza kuti mukanali ndi chidwi. Zikuwoneka kwa ine ngati Mzimu ukuyitanabe kwa winawake.

<sup>226</sup> Wokonedwa Mulungu, Inu Amene Mumadziwa zinthu zonse. Ndipo Inu amene munapanga zinthu zonse kwa cholinga cha zinthu zonse, pakuti, ena amayenera kuti adzatsutsidwe, ena amayenera kuti adzachititsidwe khungu; ena, “monga wowumba amene anawumba mbiya,” monga Paulo ananena, “wina ku ulemu, ndi wina ku manyazi.” Mmodziyo anachititsidwa manyazi, anali kungosonyeza amene ankeyenera kupatsidwa ulemu. Koma kodi izo siziri m’dzanja la Woumba kuchita chimene Iye akufuna? Kodi izo siziri mu dongosolo lokonzedweratu la Mulungu, kuti ayitane? “Amene Iye anawadziwiratu, Iye anawayitana. Iwo Amene Iye anawayitana, Iye anawalungamitsa. Ndipo iwo Amene Iye anawalungamitsa, Iye wawapatsa ulemelero.”

<sup>227</sup> Mwinamwake ena a iwo pano lero ali ngati mkazi wamng’ono pa chitsime, kuchoka mu nyansi, kuchoka mu kusakhulupirira, kuchoka mu miyambo ya anthu, ziphunzitso zopangidwa ndi anthu. Mwinamwake nthawi yoyamba imene iwo anamvapo zinthu zimenezi, koma chinachake chachenjeza mwachirendo mmitima yawo. Alipo ambiri, manja ambiri

akwezedwa mmwamba, Ambuye. Mulole Woumba wamkuluyo atenge chotengeracho tsopano ndipo achiwumbe icho kukhala chotengera chaulemu. Ine ndikukhulupirira kuti pali chifukwa china, Ambuye, kapena iwo sibwenzi akuchita zimenezo, iwo sakanati azinena zimenezo. Ine ndikukhulupirirabe, ine ndikuwagwirizira iwo.

<sup>228</sup> Mulole wantchito Wanu wodzichepetsa achonderere, Ambuye. Tiloleni ife tiwachonderere iwo, monga mmodzi woyima pakati pa amoyo ndi akufa; monga mmodzi amene mu Sodomu ankachonderera anthu a ku Sodomu, “Tulukani mmenemo! Tulukani mmenemo, mwamsanga!”

<sup>229</sup> Mulole iwo abwere, Ambuye, modzichepetsa ndi mokoma ku mpandowachifumu wa Mulungu tsopano, mu mtima mwawo, akuti, “Yesu, kuyambira lero, mpaka mtsogolo, Inu mukhale wanga. Ine ndikupanga lonjezo ili kwa Inu tsopano apa, pamene ine ndakhala pano pa mpando uwu pamene Mzimu Wanu wandikhudza ine. Ngati Iwo unandikhudza ine pano, ine sindikuyenera kuti ndipite patsogolo kuposa apa. Pomwe pano ndi pamene Inu munakomana nane; pomwe pano ndi pamene ife titakonze izo; pomwe pano pa mpando wachiwiri uwu, mpando wachitatu, mpando wachisanu, chirichonse chomwe icho chiri. Pomwe pano ndi pamene izo ziti zikonzedwe, chifukwa pano ndi pamene Inu munanditsutsa ine, pano ndi pamene Inu munalonjeza kuti mudzakonza izo. Pakuti ngakhale ndingakhale wodetsedwa ndi wauve, ndidzayeretsedwa ngati chipale. Ine ndidzakhulupirira Mawu Anu onse. Ndine wokonzeka kuyenda mu Iwo, kuwakhulupirira Iwo, kuwalandira Iwo.

“Ndipo ine tsopano ndikuchita izi kwa ulemelero wa Mulungu, podziwa kuti moyo wanga siwabwino kwa ine, siwabwino kwa Mulungu, siwabwino kwa anansi anga, siwabwino kwa china chirichonse; basi mophweka wabwino kwa mdierekezi, kuti azindipanga a—kukhala chidole, kuti azindiponyera paliponse, mwinamwake kukhala choseweretsa cha mwamuna wina kuti azichiyang’ana, mwinamwake fano la mkazi wina. Mulungu, ndipangeni ine ndikhale wantchito kwa Inu.” Perekani izi, Ambuye. Ine ndikuwapereka iwo kwa Inu tsopano, mu Dzina la Yesu Khristu, Mwana Wanu.

Ndi mitu yathu yoweramitsidwa, ndi mitima yathu.

Ndikutha kumva Mpulumutsi wanga . . .

Moona mtima, mzanga. Ikhoza kukhala nthawi yanu yomaliza. Kodi inu mukulumva Liwu laling’onolo?

. . . akuyitana,  
Ine ndikukhoza . . .

Kodi Iye akuyi- . . .? Nchiyani chikukuitanani inu, ngati Mpulumutsi wanu ali? Mawu.

. . . Mpulumutsi akuyitana,

Kodi mukuyenera kuchita chiyani? Kulikana dziko.

Ndipo tenga mtanda wanga ndi kunditsatira,  
kunditsatira . . .

“Ine ndanyalanyaza ubatizo mu Dzina la Yesu, Ambuye.”

Ndidzapita Naye m’mundamo,  
Ndidzapita . . .

Ndi Iye, kuti? Kudutsa m’madzi, kudutsa m’munda,  
kudutsa paliponse; nyumba ya pemphero, mu dziwe, kulikonse.  
Kusankha izo!

. . .pita Naye kudutsa mmunda,  
Ine ndidzapita Naye, Naye mnjira yonse.

Ndidzapita Naye mu chiweruzo,

Kaya Mawu ndi olondola kapena mpingo ndi wolondola.

Ndizda . . .

“Kaya ndi kulondola, kapena Iye akulondola. Kodi chikumbumtima changa chikulondola, kapena Mawu Ake ndi owona?” Inu muli mmalo achiweruzo tsopano. “Chimene ndakhulupirira, kodi ndi cholondola, kapena Mawu Ake ndi olondola? Kodi ndikuganiza kuti ndibwino kukhala ndi tsitsi lalifupi, kuvala akabudula? Kodi ndikuganiza kuti zolondola kukhala wachipembedzo?” Kodi Iye ananena chiyani?

Ine ndidzapita Naye, Naye njira yonse.

Tsopano kumene Iye anditsogolera  
ndidzamsatira,

Ine ndakweza manja anga mmwamba, inenso, Ambuye. Ambuye, kaya ndi kuti, Uthenga wotsatira ukalalikidwa kuti? Kodi ndi kuno, usikuuno, uko mu Afrika, Germany, Switzerland? Iwo uli kuti, Ambuye?

Kumene Iye . . .

Kulikonse kumene Inu mutsogolera, Ambuye.

. . .ine ndidzatsatira,  
Ndinka Naye, Naye njira yonse.

Tsopano ndi mitu yanu yoweramitsa.

<sup>230</sup> Kodi mupita Naye kulikonse kumene Iye akukutsogolerani? Kodi mupita ndi Iye pamene nthawi ikucheperachepera, anthu akuzunza, akukusekani, akukuserewulani? “Ine ndidzakhale ndi Iye. Ine ndidzapitabe. Ine ndidzasunthirabe chitsogolo ndi Inu, Ambuye, kulikonse kumene Inu muli. Ndidzakhale wokhulupirika ndi woona. Mu kutantha kwa nkondoyi, ndidzakhale wokhulupirika ndi woona. Ngati ine ndigwa, Inu mudzandidzutsanso, Ambuye. ‘Iye amene ataya moyo wake chifukwa cha Ine adzawupeza iwo.’”

Chotero ndidzapita ndi Iye, ndi Iye yonse. . .

<sup>231</sup> Tsopano onse amene akutanthauza zimenezo, kuchokera mu mtima mwanu, tiyeni tikweze manja athu tsopano, ndi mitima yathu, kwa Iye.

Ine . . . Kumene Iye anditsogolera  
ndidzamsata,

Kumene Iye anditsogolera ndidzamsata,  
Kumene Iye anditsogolera ndidzamsata,  
Ndidzapita Naye, Naye njira yonse.

Iye adzandipatsa chisomo ndi ulemelero,  
Iye adzandipatsa ine. . .

Ambuye Yesu, pumirani pa mipango iyi tsopano. Muwachize odwala ndi osautsika awa, Ambuye. Perekani izi, Ambuye. Apatseni iwo machiritso, Ambuye, mu Dzina la Yesu.

Ndipo kupita ndi ine, ndi ine njira yonse.

<sup>232</sup> Inu mukumverera bwino tsopano? Mukumverera kuti zonse zakonzeka tsopano? Ngati Iye. . .

Lipenga la Ambuye lidzawomba, ndipo  
nthawi sidzakhala ponso, (Limenelo ndi  
Lipenga lotsiriza lija, tsopano.)

Ndipo pamene mmawa ukutulukira ku  
Muyaya, wowala ndi wokongola.

Tiyeni tiyimbe iyo, tonse a ife tsopano. “Pamene Lipenga la Ambuye lidzawomba.” Tipatseni ife poyambira.

Pamene Lipenga la Ambuye lidzawomba,  
ndipo nthawi sidzakhala ponso,  
Ndipo mmawa ukutulukira ku Muyaya,  
wowala ndi wokongola;

Pamene opulumutsidwa a mdziko  
adzasonkhana kutsidya M’mphepete mwa  
nyanja,

Pakuitana dzina langa, ndidzakhala komweko.

Pakuitana dzina langa,  
Pakuitana dzina langa,  
Pakuitana dzina langa,  
Pakuitana dzina langa, ndidzakhala komweko.

Mmawa wowala ndi wopanda mitambo  
pamene akufa mwa Khristu adzauka,  
Ndi kugawana ulemelero wa kuuka Kwake;  
Pamene moyo wonse watha, ndipo ntchito  
yathu padziko yatha,  
Ndipo pakuitana, ndidzakhala komweko.

Pakuitana dzina langa,  
Pakuitana dzina langa,  
Pakuitana dzina langa,

Pakuitana dzina langa, ndidzakhala komweko.

<sup>233</sup> Tiyeni tikweze manja athu, tinene, “Mwa chisomo Chanu, Ambuye.” “Mwa chisomo Chanu, Ambuye!”

Tsopano, ndife abale ndi alongo mwa Khristu. Tiyeni tingotembenuka ndi kungogwirana chanza ndi winawake pafupi nanu, ndikuti, “Mwa thandizo la Mulungu, pamene adzayitana dzina kumeneko!”

Pakuitana dzina langa,  
Pakuitana dzina langa,  
Pakuitana dzina langa,  
Pakuitana dzina langa, ndidzakhala komweko.

Kodi tikuyembekezera chiyani?

Pamene Lipenga limenelo. . . (womalizayo). . .  
Ambuye lidzawomba, ndipo nthawi  
sidzakhhalapo. . .  
(Yatha kulowa mu Muyaya, “Mkamphindi,  
mkuthwanima kwa diso.”). . . ndi kokongola;  
Ndipo pamene opulumutsidwa apa dziko  
adzasonkhanitsidwa, ku gombe linalo,  
Pakuitana dzina langa, ndidzakhala komweko.

Tiyeni tingoiyimba iyo!

Pakuitana dzina langa,  
Pakuitana dzina langa,  
Pakuitana dzina langa,  
Pakuitana dzina langa, ndidzakhala komweko.

<sup>234</sup> Oh, kodi iyo siidzakhala nthawi! Kumangoyenda, tsiku lina, ndipo apa pawonekera winawake. “Kodi ndi ndani? Amayi!” Amen! “Sizitenga nthawi yaitali tsopano.” Mu maminiti pang’ono chabe, inu mudzasinthidwa. Ndipo ife tidzakhala. . . tidzakumana nawo, kenako nkudzatengedwera mmwamba limodzi ndi iwo, kukakomana ndi Ambuye mu mlengalenga. Oh, mkamphindi, nkuthwanima kwa diso. Kudzati, “Apa pali M’bale Seward, m’bale wachikulire yemwe ankakhala ku tchalitchi pa pano! Bwanji, apa pali M’bale DeArk. Apa pali M’bale *Wakuti*- . . . Bwanji, taonani apa, iwo onse ali mondizungulira ine! Vuto ndi chiyani? Pano mu maminiti pang’ono chabe. . . Ndikudziwa kuti iwo anawonekera kwa ine. Sizitenga nthawi yaitali tsopano. Ine ndidzasinthidwa tsopano, mkamphindi chabe, mphindi chabe.” Oh, inde! Ndipo m’mawa ukutulukira ku Muyaya, wowala ndi wokongola. Mitambo yonse ya chifunga. . .

<sup>235</sup> Monga Iye anati, “Israeli, iwe wakhala ngati mtambo wa m’mawa, nthunzi, ndipo chirungamo chako chazimirira.” Ndipo pamene zonse zazimirira mu Kuwala kwa Mwana Amene amagwira izo zonse, ameni, ndiye, “Pakuitana dzina, ine ndidzakhala komweko.” Chabwino.

Mpaka usikuuno:

Mpaka tidzakumane! mpaka tidzakumane!

Sitikudziwa nthawi yomwe izi ziti zidzachitike, abwenzi. Yakhala nkhani, nthawi yayitali, koma ndi Choonadi, ndipo izo zidzachitika. Ife tiri pa nthawiyo tsopano.

Mpaka—mpaka tidzakumane! mpaka ife. . .

Mwa chisomo cha Mulungu, ife tikuyembekeza, hafu pasiti seveni usikuuno.

Mulungu akhale nanu mpaka tidzakomanenso.

Tiyeni tiyime tsopano pa mapazi athu.

<sup>236</sup> Oh, kodi izo si zodabwitsa? “Awa ndi malo Ammwambamwamba mwa Khristu Yesu.” Sitingasinthanitse izi ndi chirichonse. Inu mukudziwa momwe ine ndimakondera kuwedza ndi momwe ine ndimakondera kusaka, chifukwa ine ndimamuwona Mulungu kunja uko mu chipululu. Ndimakonda izo. Koma, oh, ine sindingasinthe miniti imodzi ndi izi, pa zochitika zonse za zaka mahandirede. Miniti imodzi ya izi, kukhutitsidwa kumeneko!

<sup>237</sup> Mulungu, lengani mwa ine chitsitsimutso. Ndiroleni ine ndikhale chitsitsimutso. Mulole aliyense wa ife akhale chitsitsimutso, chitsitsimutso mwa ine. Ndipangeni ine, Ambuye, kuti ndizimva njala, ndipangitseni ine kuchita ludzu. Mulenge mwa ine, Ambuye, icho chimene chikufunikira mwa ine. Mundirole ine, kuyambira ora lino mpakana, ndikhale Wanu; wantchito wodzipereka kwambiri, wantchito wabwinoko, wodalitsidwa kwambiri ndi Inu; wokhoza kwambiri, wodzichepetsa kwambiri, wachifundo kwambiri, wofunitsitsa kugwira ntchito; woyang’ana koposa zinthu zomwe ziri zabwino, ndi kuyiwala zinthu zakale, ndi zoyipa. Ndiroleni ine ndikankhire ku chilemba cha mayitanidwe apamwamba a Khristu. Amen.

Ndicho chikhumbo chatu, sichoncho icho?


Chabwino, tiyeni, mpaka tikomanenso usikuuno, tiyeni titenge Dzina la Yesu ndi ife tsopano, aliyense wa inu tsopano.

Tengani—tenga Dzina la Yesu nawe,  
Mwana wachisoni ndi watsoka;  
Lidzakusangalatsa ndi kukutonhoza iwe,  
Litenge Ilo kulikonse upita.

Dzina lofunika, O ndi lokoma bwanji!  
Chiyembekezo cha padziko ndi chisangalalo  
cha Kumwamba;  
Dzina lofunika, O ndi lokoma bwanji!  
Chiyembekezo cha padziko ndi chisangalalo  
cha Kumwamba.

Tsopano tiyeni tiweramitse mitu yathu.

Tenga Dzina la Yesu nawe,

Monga Chishango ku msampha uliwonse;  
Pamene mayesero akuzingani . . . 

64-0726M Kulizindikira Tsiku Lanu Ndi Uthenga Wake  
Branham Tabernacle  
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)



## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)